KODI BAIBULO NCHIYANI?

"BAIBULO," "MALEMBO OYERA," KAPENA "MAU A MULUNGU," NDI BUKU LOMWE LILI MAZIKO A CHIKHULUPIRIRO CHA CHIPEMBEDZO CHA CHIKHRISTU. BUKU LIMENELI NDI LOSIYANA NDI MABUKU ENA ONSE. BAIBULO LONSE LILI NDI MABUKU 66 AMENE ADALEMBEDWA NDI ANTHU PAFUPIFUPI 40, OCHOKERA KU ASIYA. ANTHU AMENEWA ANKAGWIRA NTCHITO ZOSIYANASIYANA; ENA ADALI MAFUMU, OKHOMETSA MSONKHO, ASODZI, MADOKOTALA, ALIMI, ANTCHITO ZOLEMBEDWA, MALOYA, NDI ENA OTERE. ANTHU AMENEWA ADALEMBA BAIBULO KWA ZAKA PAFUPIFUPI 1500. AMBIRI MWA ANTHUWA SANKADZIWANA NDIPO ANKAKHALA M'MALO OSIYANASIYANA, KOMABE PAMENE MABUKU A M'BAIBULO ANKASONKHANITSIDWA PAMODZI, MABUKUWO ANALI NDI TANTHAUZO LIMODZI NDIPO ANKAKAKAMBA NKHANI IMODZIMODZI. IZI ZILI CHONCHO CHIFUKWA MZIMU WOYERA NDIYE ANKATSOGOLERA ANTHU OSIYANASIYANAWO KUTI ALEMBE ZIMENE IYEYO ANKAFUNA KUTI ZILEMBEDWE. TERE BAIBULO NDI BUKU LAKALEKALE LOMWE NDI LOTCHUKA KWAMBIRI NGAKAHLE MASIKU ANO. BAIBULO NDI BUKU LOYAMBA KUSINDIKIZIDWA M'MALO OSINDIKIZIRA MABUKU NDIPO LATANTHAUZIDWA M'ZIYANKHULO ZAMBIRIMBIRI.

בראשית ברא אלהים את השמים ואת הארץ

CHIPANGANO CHAKALE CHIMENE TIKUNENACHI NDI BAIBULO LIMENE NGAKHALE AYUDA AKUGWIRITSABE NTCHITO MPAKA LERO LINO.

CHIPANGANO CHATSOPANO CHILI NDI MABUKU 27, MACHAPUTALA 260. ONSE AMENE ADALEMBA CHIPANGANO CHATSOPANOCHI ANKAGWIRITSA NTCHITO CHINENERO CHA CHIGRIKI CHOMWE CHIMAONEKA CHONCHI:

εν αρχη ην ο λογος και ο λογος ην προς τον θεον και θεος ην ο λογος

BAIBULO LIMANENA MBIRI YOONA YA DZIKO LAPANSI NDIPO LIMANENERATU ZA CHIMALIZIRO CHA DZIKOLI. LIMAKAMBA ZA CHIYAMBI CHA ANTHU, GWERO LA TCHIMO, NDIPO LIMAKAMBANSO ZA KUMWAMBA NDI GEHENA.

CHIMENE CHIMAONETSA KUTI BAIBULO SIBUKU WAMBA NKUTI BUKULI LAKHALA LIKUNENERATU ZAKUTSOGOLO NDIPO ZONENEDWERATUZO ZAKHALA ZIKUCHITIKA NDITHU.

BAIBULO LILI NDI MAYANKHO OYENERA PA MAFUNSO ANU AMENE MUNGAKHALE NAWO, MONGA:

NCHIFUKWA CHIYANI TILI PANO? CHOLINGA CHATHU NCHIYANI?
NCHIFUKWA CHIYANI, TITABADWA M'DZIKO LAPANSILI, TIMAFA?
NANGA TIKAMWALIRA, MIZIMU YATHU IMAPITA KUTI?
TIKAMWALIRA, KODI TIDZABADWANSO NGATI CHINA CHAKE?
KODI ZIWANDA ZIMASIYANA BWANJI NDI MIZIMU YA ANTHU AKUFA?
NCHIFUKWA CHIYANI ANTHU AMASIYANA NDI NYAMA?
KODI KWENIKWENI TCHIMO NCHIYANI?
KODI TIYENERA TICHITE CHIYANI KUTI TIPULUMUTSIDWE KU TCHIMO NDI KU IMFA?
KODI NZOONADI KUTI KULI MULUNGU?

NCHIFUKWA CHIYANI MUNTHU AMAZUNZIKA, KUKHUMUDWA, KENAKA NKUFA?

MUTU

1. CHIYAMBI 1
2. ABRAHAMU 21
3. MOSE 36
4. EKSODO 65
5. ANENERI 95
6. UNENERI WOKHUDZA KHRISTU 141
7. CHIPANGANO CHATSOPANO, KUBADWA KWA KHRISTU, NDI MAYESERO AKE 157
8. UTUMIKI WOYAMBIRIRA 177
9. ZOZIZWITSA NDI MAFANIZO 208
10. PASKHA NDI MASAUTSO A KHRISTU 241
11. KUUKA KWA AKUFA, PENTEKOSTE NDI MPINGO WOYAMBIRIRA 271
12. KU DZIKO LONSE LAPANSI 299

ZABWINO NDI ZOIPA®

COPYRIGHT © 2006 BY MICHAEL AND DEBI PEARL

LINASINDIKIZIDWA NDI:
NO GREATER JOY MINISTRIES, INC.
1000 PEARL ROAD
PLEASANTVILLE, TN 37033
WWW.NOGREATERJOY.ORG

WOTANTHAUZIRA BUKULI M'CHICHEWA NDI:
BISWICK CHIMBALU NKHOMA
ZOMBA THEOLOGICAL COLLEGE
P.O. BOX 130
ZOMBA

MUTU 1:
CHIYAMBI



ONANI TSAMBA 321 PAMENE AKULONGOSOLA MWACHIDULE ZA BUKU LOTCHEDWA BAIBULO. KUTI MUDZIWE ZAMBIRI ZA SATANA ONANI YESAYA 14:12-14, 45:18; EZEKIELE 28:13-19; MATEYU 25:41; LUKA 10:18; CHIVUMBULUTSO 12:4, 20:2



MWINA 4004 B.C. – GENESIS 1:2-3

GENESIS 1:31, 2:7

GENESIS 1:28; 2:2, 16–22, 25

GENESIS 3:1–6; CHIVUMBULUTSO 20:2

GENESIS 3:6-12

MULUNGU ANAFUNSA HAVA ZIMENE ZIDAACHITIKAZO NDIPO HAVA ADAYANKHA KUTI:

SIIIII...

NJOKA NDIYO IDANDINYENGA. IDANDIUZA KUTI SINDIDZAFA, KUTI NDIDZAKHALA WOFANANA NANU, KOMA SINDINE WOFANANA NANU. NDIKUDZIMVERA CHISONI.

CHONCHO MULUNGU ADATEMBERERA NJOKA NATI KWA IYO

POPEZA WACHITA ZIMENEZI, UZIDZAYENDA NDI MIMBA YAKO NDIPO FUMBI LIDZAKHALA CHAKUDYA CHAKO.

NDIPO NDIDZAIKA UDANI PAKATI PA MBEU ZAKO NDI MWANA WA MKAZIYU. MBEU ZAKO ZIDZALUMA CHIDENDENE CHA MWANA WA MKAZIYU, KOMA IYE ADZAPHWANYA MUTU WAKO.

PANO MULUNGU AKUKAMBA ZA NKHONDO YAM'TSOGOLO. NTHAWI IDZAFIKA PAMENE MBEU YA MKAZI IDZAGONJETSA SATANA. MUNTHU AMENEYO ADZAOMBOLA ANTHU NDI KUWAYANJANITSANSO NDI MULUNGU NDIPO ADZAWAPULUMUTSA KU TEMBERERO LA TCHIMO NDI IMFA.

MULUNGU AKADATHA KUONONGA LUSIFARA NDI ANGELO AKE MKAMPHINDI KOCHEPA. KOMA ADAWALEKA NDI MOYO KUTI AZIYESA ANTHU. KODI ANTHU ADZAMVERA MULUNGU, KAPENA ADZATSATA SATANA WOGALUKIRAYO?

GENESIS 3:13-15

GENESIS 3:17-24; EZEKIELE 18:4

GENESIS 4:1-4; AROMA 3:23; AHEBRI 11:4

AI, KAINI
MULUNGU ANAKANA NSEMBE YA KAINI CHIFUKWA INALIBE MAGAZI.
MULUNGU ADAKONDWERA NDI ABELE CHIFUKWA CHA NSEMBE YAKE. PAMENE MULUNGU ADAONA MAGAZI A NKHOSA YOSALAKWA, ADAKHULULUKIRA ABELE.
MULUNGU ADATI KWA KAINI, "UKACHITA ZABWINO, NDIDZAKONDWERA NAWE. KOMANSO UDZALAMULIRA MBALE WAKO ABELE NDIPO ADZAKHALA PANSI PA ULAMULIRO WAKOWO."
KODI UKUGANIZA KUTI NDIWE WOPAMBANA? ZIPATSO ZANGA NDI NDIWO ZAMASAMBA ZINALI ZOPOSA NKHOSA YAMAGAZIYO. KODI CHIKUKUCHITITSA KUKHALA WOPAMBANA NCHIYANI? KODI IWE NDIWE WABWINO KUPOSA INE?
MBALE WANGA, NTHAWI IKADALIPO NDIPO UKHOZA KUPEREKA NSEMBE YAMAGAZI.
USANDITAYITSE NTHAWI! SINDIDZAKUMVERA NSO!
KHOO!
ABELE ANAPHEDWA, NDIPO KAINI ANKAYESA KUBISA TCHIMO LAKE LAKUPHALO.

GENESIS 4:5-8

GENESIS 4:9-16, 5:4; MACHITIDWE 17:24-26

GENESIS 6:5-7; AROMA 5:12



GENESIS 6:8-9, 17-22, 7:2



GENESIS 7:7–9; 2 PETRO 2:5

GENESIS 7:9–11, 16

GENESIS 7:12, 19–23, 8:9–11

POSAKHALITSA BWATO LIJA LINABWATAMA PAMWAMBA PA PHIRI LOTCHEDWA ARARATI. ALIYENSE ADATULUKIRA KU DZIKO LATSOPANO-DZIKO LOPANDA UCHIMO.

NOWA ANAMANGA GUWA LANSEMBE NAPEREKERAPO NSEMBE ZA NYAMA. NGAKHALE NOWA ANALI WOLUNGAMA, MUMTIMA MWAKE MUNALI UCHIMO NDITHU. NSEMBE ZAMAGAZIZI ZINKAPEREKEDWA KWA MULUNGU M'MALO MWA MOYO WA NOWA NDI BANJA LAKE.

NYAMA ZISANU NDI ZITATU ZIKUIMIRA ANTHU ASANU NDI ATATU AMENE AKANAFA NDI CHIGUMULA CHIJA KOMA ANAPULUMUKA CHIFUKWA CHA CHISOMO CHA MULUNGU. ZIKUFANANAKO NDI ZIMENE MULUNGU ADACHITA M'MUNDA WA EDENI MUJA PAMENE ADAPHA NYAMA NDI KUPANGIRA ZOVALA ZA ADAMU NDI HAVA.

NDIDZAIKA UTAWALEZA MUMLENGALENGA KUTI UKHALE CHIZINDIKIRO CHAKUTI SINDIDZAONONGANSO DZIKO LAPANSI NDI MADZI. MUKHALE NDI ANA AMBIRI NDIPO MUMWAZIKANE NDI KUDZAZA DZIKO LAPANSI.

NDIDZACHITITSA KUTI NYAMA ZIZIOPA ANTHU. MUYENERA KUDYA CHOLENGEDWA CHILICHONSE CHAMOYO NDI CHOKWAWA PA DZIKO LAPANSI, MONGA MOMWE MUMADYERA NDIWO ZAMASAMBA NDI ZINA ZOTERE. KOMA MUSADYE MAGAZI A CHOLENDEDWA CHILICHONSE. MUSAPHE MUNTHU ALIYENSE.

NGATI WINA WAPEZEKA NDI MLANDU WOPHA MNZAKE ANTHU ENA AYENERA KUMUPHA. NGATI MUNTHU AKHETSA MWAZI WA MNZAKE, ANTHU ENA AYENERA KUKHETSA MWAZI WAKE KUTI ALIPIRE MLANDU WAKE, CHIFUKWA MOYO ULI M'MWAZI.

NOWA ANALI MLIMI NDIPO ANABZALA MPESA. PA DZIKO LAPANSI PANALI MABANJA ANAI OKHA. KOMA KENAKA ANA A NOWA ANAYAMBA KUBEREKA ANA AONSO.

NOWA ADAONA KUTI AKAIKA CHIPATSO M'KONTENA NDI KUCHISIYA OSACHIDYA KWA MASABATA ANGAPO, CHIMAPANGA CHAKUMWA CHOLEDZERETSA CHIMENE AMATI AKAMWA CHIMAMPATSA CHIMWEMWE. NOWA ADAYAMBA KUKONDA CHAKUMWACHO NDIPO NTHAWI ZINA SANKATHA KUGWIRA NTCHITO. ANKAGONA NGATI WAFA. CHINKAMUCHITITSA ZINTHU ZOSAKONDWERETSA MULUNGU.

GENESIS 8:4, 20, 9:1-29



GENESIS 9:21–27; 1 MBIRI 4:40; SALIMO 78:51, 105:23, 27, 106:22

GENESIS 10:6–10, 11:1–9

MUTU 2: ABRAHAMU



GENESIS 12:1-3, 13:14-17

GENESIS 15:1-6, 13-14

GENESIS 16:1-4

GENESIS 16:4-16

ISIMAELE ANABADWA PAMENE ABRAHAMU ANALI NDI ZAKA 86. ATABADWA ISIMAELE, POSAKHALITSA, ABRAHAMU ANAKALAMBA KWAMBIRI NDIPO ZINALI ZOKAIKITSA KUTI NKUBEREKANSO. KODI ISIMAELE NDIYE MWANA AMENE MULUNGU ANALONJEZA ABRAHAMU? KOMA MULUNGU ANATI MWANA WALONJEZOYO ADZABADWA KUPYOLERA MWA SARA NDI ABRAHAMU.

KODI MULUNGU ADZAKWANIRITSA BWANJI LONJEZO LAKE POPEZA SARA NDI ABRAHAMU NGOKALAMBA KWAMBIRI, OSAYEMBEKEZEKA KUBALA ANA.

PAMENE ISIMAELE ANALI NDI ZAKA 13, ABRAHAMU ALI NDI ZAKA 99, MULUNGU ANAYANKHULA NAYENSO ABRAHAMUYO.

ABRAHAMU, INE NDINE MULUNGU WAMPHAMVUZONSE. CHITA ZONSE ZIMENE NDIKUKUUZA NDIPO USACHIMWE. MONGA NDINAKUUZAKALENDIDZACHULUKITSA ANA AKO, NDIPO IWEYO UDZAKHALA TATE WA MAFUKO AMBIRI. //NDIDZAKHAZIKITSA PANGANO LANGA NDI IWE KOMANSO NDI ANA AKO A PAMBUYO PAKO.

NDIDZAPEREKA DZIKO LA KANANI NGATI CHOLOWA KWA ANA AKO MPAKA MUYAYA. SARA ADZAKHALAWOYEMBEKEZERA NDIPO ADZABALA MWANA MONGA NDINALONJEZERA, MWANAYO NDIYE ADZAKHALE MTSOGOLERI WA MAFUKO AMBIRI.

HA-HA. ZIMENEZI ZINGATHEKE BWANJI? INE PANO NDILI NDI ZAKA 99, NDIPO SARA ALI NDI ZAKA 89. THUPI LANGA LILI NGATI LA MUNTHU WAKUFA. SITINGABEREKE. CHONDE MULOLE KUTI ISIMAELE AKHALE MWANA WALONJEZO.

AI, MONGA NDIDANENERA PACHIYAMBI PAJA, IWE NDI SARA MUDZAKHALA NDI MWANA WANUWANU, WOTULUKA M'THUPI LANU. LONJEZO LA MADALITSO LIDZAPITIRIRA KUPYOLERA MWA IYE, OSATI ISIMAELE. CHAKA CHINA SARA ADZABEREKA MWANA WAMWAMUNA.

NZOTHEKA?..... INDE. MULUNGU AMENE ANALENGA THUPI LA MUNTHU, AKHOZA KUTENGA MATUPI AWIRI OKALAMBA, MATUPI ONGA A ANTHUAKUFA, NDI KUWAPATSANSO MPHAMVU ZOBEREKERA.....ZOONADI. MULUNGU AKHOZA KUCHITA CHINTHUCHOTERE!

PATAPITA MASIKU ANGAPO, ANTHU ATATU OCHOKERA M'CHIPULULU ANAMUWONEKERA ABRAHAMU. SANKAWONEKA NGATI AYENDA MTUNDA WAUTALI, KOMANSO SANALI ANTHU OCHOKERA M'MIDZI YOYANDIKANA NDI ABRAHAMU. ANALI AMPHAMVU, ODALIRIKA, NDI ACHIKHALIRE.

ABRAHAMU ADAWAYANG'ANITSITSA AKUYANDIKIRA NDIPO ANADZIWA KUTI ANALI ANTHU OSIYANA NDI ANTHU ENA, KOMA SANKADZIWA KUTI ALENDO AKEWO SANALI OCHOKERA M'DZIKO LINO LAPANSI.

AWIRI A IWO ANALI ANGELO OLUNGAMA, KOMA WACHITATUYO ANALI MULUNGU AMENE ANKAWONEKANSO NGATI MNGELO NKUMAYANKHULA NDI ABRAHAMU. ABRAHAMU ANAPITA KUKAWALONJERA.

GENESIS 17:1-21, 18:1-2

GENESIS 18:10-22

GENESIS 18:23–19:2

GENESIS 19:4–17

GENESIS 19:24–26; LEVITIKO 18:22; AROMA 3:23–32, 6:23; 1 AKORINTO 6:9–11; CHIVUMBULUTSO 21:8

GENESIS 21:1-3, 9-14 *DZINA LOTI ISAKE LIMATANTHAUZA KUTI KUSEKA

GENESIS 22:2; AROMA 5:12

GENESIS 22:3-9

GENESIS 22:9–18; AHEBRI 11:17–19



GENESIS 21:5, 13, 24:67, 25:12-18, 21-26, 29:23-30

MUTU 3:
MOSE



GENESIS 46:5–7; EKSODO 1:1–12, 22

KOMA AMAI, NDIDZAWAUZA CHIYANI ASILIKALI NDI ANZATHU ENA AKAFUNSA KUTI KHANDA LATHU LILI KUTI?
UDZAWAUZE ZOONA ZOKHAZOKHA. AMAI AKE ANANTAYA MU MTSINJE KOTERO KUTI ASILIKALI SANAMUPHE.
PAFUPIFUPI 1525 B.C.
AMAI, KODI M'MENEMU SIMULOWA MADZI?
TACHIMATA NDI PHULA. CHIZIDZAYAN DAMA.
KODI TIDZAMUONANSO MCHIMWENE WATHUYU? ONANI AIGUPTOWO!
MULUNGU ADZAMUTETEZA. IWE UKAKHALE PAFUPI POMWEPO NDIPO UZIKAMUYANG'ANIRA.
MWANA WAMKAZI WA FARAO ANABWERA KUMTSINJEKO KUDZASAMBA.
TAMVEARNI! NDIKUMVA KULIRA KUCHOKERA MU MTANGA UWO!
EEE, NDI WOKONGOL A ETI?
AYENERA KUKHALA MMODZI MWA ANA A AHEBRI.
AYENERA KUTI ALI NDI NJALA.
NDIKANAPEZA WINA WOTI AZINDIYAMWITS IRA NDIKADAMUSUNG A MWANAYU.
MMODZI MWA ANA A AHEBRI ALI PANO. MWINA MWAKE ANGADZIWE WINA WOTI NKUMAYAMWITSA MWANAYU.
NDIPITA KUTI NDIKAYESE KUPEZA MAI AMENE AKHOZA KUYAMWITSA MWANAYU. NDIKUDZIWA KUTI PALI WINA AMENE WANGOTAYA MWANA WAKE MU MTSINJE. AMENEYO AKANALI NDI MKAKA WAMBIRI M'MAWERE AKE.

EKSODO 2:3-9

NDACHITA CHIYANI? KODI NDIDZAMUONANSO MWANA WANGA? KODI MULUNGU AMASAMALADI?
MUKANACHITA CHIYANI? SIMUKANAMUBISA MPAKA KALE KALEKALE. NDITHU, ASILIKALI AKANAMUPEZA NDI KUMUPHA. MUYENERA KUNGOKHULUPIRIRA MULUNGU.
AMAI, AMAI!
AMAI, MWANA WAMKAZI WA FARAO ANABWERA KU MTSINJE NDIPO WAPEZA MCHIMWENE WANGA WAMNG'ONO UJA. AFUNA KUTI MWANAYO AKHALE WAKE, NDIPO AKUFUNA MAI WINA WOTI AZIMUYAMWITSIRA! NDIPO TSOPANO AKUBWERA KUNYUMBA KUNO!
ADALITSIKE MULUNGU WAMUYAYA!
NDAMVA KUTI MWANA WANU ANAPHEDWA. PEPANI KWAMBIRI. MWANA UYU NDAMPEZA MU MTSINJE. MUZINDIYAMWITSIRA NDIPO NDIDZAKULIPIRANI. //
AKADZALEKA KUYAMWA NDIDZABWERA KUDZAMUTENGA NDI KUPITA NAYE KU NYUMBA YACHIFUMU KUMENAKALEREDWE KUTI ADZAKHALE FARAO WA DZIKO LA EJIPITO. TIDZAMUTCHA DZINA LAKE MOSE.
PAMENE MOSE ANKAKULA, MAI WAKE UJA ADAMUPHUNZITSA ZA MULUNGU WOONA WA MAKOLO AKE. MULUNGU ANALI NDI CHOLINGA CHAPADERADERA NDI MWANA AMENEYU.
LUMPHIRA MUNO, MWANA WA MFUMU, TIKUPITA KU NYUMBA YACHIFUMU.
KODI ZIMENEZI ZIMATHAMANG A KWAMBIRI NDITHU?
ZIKOMO KWAMBIRI CHIFUKWA CHOYAMWITSA MOSE. AKUONEKA WATHANZI ZEDI. AKAKULA ADZAKHALA WAMPHAMVU NDI WOLEMERA.

EKSODO 2:8-10

EKSODO 2:10–11

EKSODO 2:11-15

EKSODO 2:16–3:10

EKSODO 4:1-4, 12-16

EKSODO 4:29-31

EKSODO 4:17, 30

PALIBE CHIMENE CHASINTHA M'DZIKO MUNO CHICHOKERE INE ZAKA 40 ZAPITAZO. UKUMBUKIRE KUNENA ZIMENE NDAKUUZAZI.
MULUNGU WA ISRAELE WAYANKHULA NDI MOSE. MULUNGU AKUTI ULOLE KUTI ANTHU AKE APITE M'CHIPULULU KWA MASIKU ATATU, KUKAPEMBEDZA NDI KUKAPEREKA NSEMBE.
HA! MULUNGU WA ISRAELE? HA HA HA HA, SINDIMDZIWA MULUNGU WANU. KODI MULUNGU AMENEYU NDANI KUTI NDIMUMVERE? ZIMENEZI NDI ZOSEKETSA NDITHU. SINDIDZALOLA KUTI AKAPOLO ANGA APITE M'CHIPULULU KWA MASIKU ATATU.
NDAMVA MMENE IWE UKUSOKONEZERA ANTHU ANGA, UKUWAUZA KUTI ALEKE KUGWIRA NTCHITO. NDIPO TSOPANO AFUNA ACHOKEPO KWA MASIKU ATATU KUKAPEMEBDZA MULUNGU AMENE INE SINDIMDZIWA. NDIONETSETSA KUTI NTCHITO YAO IPOSE KALE.
KUCHOKERA TSOPANO AZIDZIPEZERA OKHA UDZU WOUMBIRA NJERWA. TSOPANO CHOKANI PAMASO PANGA NDIPO BWERERANI KUMENE MWACHOKERA.

EKSODO 5:1-7

EKSODO 5:10-23, 7:7-11

EKSODO 7:11-12


ONANI! NJOKA YAKE IFUNA KUMENYANA NDI ZATHU.
NJOKA YAKE IKUDYA IMODZI MWA NJOKA ZATHU!
YAMEZERATU NJOKA YATHU!
KOMA SINGADYENSO YACHIWIRI! MULUNGU WATHU WA NJOKA, NESERITI, ADZAKWIYA.
YEHOVA NDIMULUNGUA MENEADALENG A ZONSE. AKUTI,
ZIMENEZI ZATHEKA BWANJI?
YEHOVA NDI MULUNGU AMENE ADALENGA ZONSE. AKUTI, "LOLA KUTI ANTHU ANGA AMUKE."

EKSODO 7:12

EKSODO 7:15–21

EKSODO 7:21–25, 8:6

NYUMBA YANGA YADZALA NDI ACHULE.
DZIKO LONSE LA IGUPTO LADZALA NDI ACHULE. MILUNGU YAKWIYA!
KODI ALI KUTI ANSEMBE ATHU? KODI SANGACHITEPO KANTHU?
EYIIIIII!
FARAO, TAMVERANI, IFE AMATSENGA TIKHOZANSO KULENGA ACHULE.
NCHIFUKWA CHIYANI AKULENGA ACHULE? KODI ACHULE AMENE MOSE WATIPATSA SADAKWANIRE? TSOPANO FARAO AKUTIONJEZERA ENA.
BWANJI OSAWALOLA KUTI APITE M'CHIPULULU MONGA MOMWE AKUFUNIRA? SITINGAPIRIRE NDI IZI.
ITANITSIRENI MOSE, MUMUUZE KUTI NDILI NDI MAU.
INDE BWANA, NDICHITA MONGA MWANENERA.
UMUPEMPHE YEHOVA KUTI ACHOTSE ACHULEWA. AKATERO, NDIDZALOLA KUTI ANTHU AKO APITE M'CHIPULULU KUKAPEREKA NSEMBE.
UTCHULE NTHAWI IMENE UFUNA KUTI ACHULEWA AFE NDIPO ZIDZACHITIKADI.
MAWA MMAWA.
ZIDZACHITIKA MONGA MWA MAU AKO, KUTI NONSE MUDZIWE KUTI PALIBE MULUNGU WOFANANA NDI YEHOVA.

EKSODO 8:7–10

EKSODO 8:13-19

EKSODO 8:20-32

MULUNGU ANATUMIZIRANSO AIGUPTO MLIRI WINA: NG'OMBE ZAO ZONSE, NKHOSA, AKAVALO, NDI NGAMIRA ZIDAGWIDWA NDI MATENDA A ZILONDA NDIPO ZINAFA. KOMA ZIWETO ZA AHEBRI ZIZIDAGWIDWE NDI MATENDAWO.
ZIWETO ZATHU ZONSE ZAFA KOMA ZANU ZILI BWINOBWINO. TATIUZANI CHIFUKWA CHAKE.
MOSE AKUTI NDI CHIFUKWA CHA MULUNGU WATHU AMENE WABWERA KUDZATIOMBOLA KU UKAPOLO WANKHANZAWU, KOMA INE NDINE MUNTHU WAMBA CHABE, SINDIZIDZIWA ZINTHU ZOTEREZI.
ANSEMBE ATHU AKUPEREKA NSEMBE KWA MILUNGU YATHU. NG'OMBE YATHU YOPATULIKA IKWIYA NDIPO ITHETSA ZIMENE ZIKUCHITIKAZI.
MUMUUZE FARAO KUTI WACHEDWA. NG'OMBE ZATHU ZONSE ZOPATULIKA ZINAFA. ANTHU AKWIYA KWAMBIRI AKAMVA KUTI MILUNGU YATHU SINAWAPULUMUTSE KWA MULUNGU WANKHANZA WA AHEBRIWA.
KODI MILUNGU YA IGUPTO ILI KUTI? KODI ILIBE MPHAMVU?
KOMA FARAO ADAUMITSABE MTIMA WAKE.

EKSODO 9:6-7

MULUNGU ANAYANKHULANSO NDI MOSE KUTI AWAZE PHULUSA PAMWAMBA PA MZINDA, NDIPO AIGUPTO ADZATULUKA ZITHUPSA M'THUPI MWAO MONSE.
MULUNGU AKUTI, "POPEZA SUKULOLA KUTI ANTHU ANGA AMUKE, NDIDZATUMIZA ZITHUPSA PA INU NDI PA ZIWETO ZANU ZONSE."
AI, ZIMENEZI ZISACHIKIKE NSO.
ITANANI AMATSENGA. AUZENI KUTI ASONKHANITSE MPHAMVU ZAO. APEREKE NSEMBE KWA MULUNGU KUTI IZI ZISACHITIKE.
MUNAITANA, INU WOPAMBANA KOPOSA?
KODI NAWENSO ULI NDI ZITHUPSA? KODI ULIBE MPHAMVU ZOTSUTSIRAMULUNGU WA MOSEYU?
CHOKERENI, INU ANTHU ACHABECHABE, OPANDA NDI MPHAMVU ZOMWE. MUMANGOPUSITSA ANTHU BASI, KOMA NDIMADZIWA KUTI NDINU ACHINYENGO. MULUNGU YANU ILI KUTI?
MULAWIRIRE MMAWA KWA FARAO KUKAMUUZA KUTI, "MULUNGU WA AHEBRI AKUTI, 'ULOLE ANTHU ANGA AMUKE. DZIWA KUTI MLIRI UMENE UKUBWERA UDZAKHALA WOOPSA KOPOSA. CHIONONGEKO CHIMENE CHIDZABWERE NDI MLIRIWO CHIDZAPHA ANTHU AKO AMBIRI. CHIFUKWA CHA CHIMENECHI UDZADZIWA KUTI KULIBE MULUNGU WINA WOFANANA NANE. SUZINDIKIRA, KOMA NDINE AMENE NDINACHITITSA KUTI UKHALE FARAO.
LIWUMA LAKOLI NDILO LACHITITSA KUTI NDIWONETSE MPHAMVU ZANGA NDI KULANGA AEJIPITO CHIFUKWA CHOZUNZA ANTHU ANGA. UKUNGOSAMALA ZAKO, NDIPO UKUKANA KUCHITA CHIFUNIRO CHANGA, TSONO MAWA NTHAWI NGATI YOMWE INO NDIDZATUMIZA MATALALA NDI MOTO, ZIMENE SIZINACHITIKEPO PA DZIKO LAPANSI.'"
NDIKUKUUZANI KUTI MUDZIWITSE ANZANU KUTI MUDZISAMALIRE PAMODZI NDI ZIWETO ZANU, SIMUYENERA KUTULUKA M'NYUMBA ZANU, ZIWETO ZANUNSO ZISATULUKE M'KHOLA, POPEZA CHILICHONSE CHIMENE CHIDZATULUKA CHIDZAFA."

EKSODO 9:8-19

EKSODO 9:23-26

EKSODO 10:14-20

EKSODO 9:26–35, 10:13–15

EKSODO 10:22-29, 11:4-5, 12:3-7

EKSODO 12:26–28, 35–36

NCHIFUKWA CHIYANI SIMUNAPHE MWANAWANKHOSA NDI KUPAKA MAGAZI AKE PA CHITSEKO CHANU?
HA, KODI NAWENSO UMAKHULUPIRIRA ZACHACHABEZI? KODI MAGAZI ANG'ONONG'ONO A PA CHITSEKO ANGALETSE BWANJI IMFA? MWANA WANGA SAKUTEKESEKA. KODI PAJA DZINA LAKO NDI YOIKIMU?
AI SIZINGATHEKE. KODI MUKUGANIZA KUTI NDINE OPUSA? ANTHU OPEPERA NDIWO AYENERA KUMAPEMBEDZA.
MULUNGU WABWINO SANGAPHE ANTHU CHIFUKWA CHOLEPHERA KUPAKA MAGAZI ANG'ONO'NG'ONO PA CHITSEKO. NANGA ANTHU AMENE SADAMVE ZIMENEZI?
ABABA, NCHIFUKWA CHIYANI USIKU WA LERO UKUSIYANA NDI USIKU WINA WONSE M'MBUYOMU?
NCHIFUKWA CHAKUTI USIKU WA LERO YEHOVA ADZATUMIZA MNGELO WOONONGA KUDZAPHA ANA AAMUNA ONSE OYAMBA KUBADWA AMENE SAKHULUPIRIRA IYE. KOMA AKAONA MAGAZI, ADZADUTSA NYUMBA IMENEYO.
CHIMENECHI NDICHO CHIYAMBI CHA MASIKU KWA IFE. CHAKA CHILICHONSE NTHAWI NGATI IMENEYI TIZIDZACHITA CHIKONDWERERO CHA PASKHA, KUKUMBUKIRA KUTI MULUNGU ADATIPULUMUTSA M'DZANJA LA FARAO.
'PASKHA' NDI MAU ACHIHEBRI, KUTANTHAUZA KUTI, 'KUDUTSA' KAPENA 'KULAMBALALA.
ABABA, MVERANI KULIRAKO! NKUTHEKA KUTI MNGELO WOONONGAYO ALI M'DERA LINO.
USAOPE. IFE TAMVERA MULUNGU. MAGAZI ALI PAMPHUTHU PA CHITSEKO. TIKUDYA MWANAWANKHOSA.
MWANA WANGA WAMWAMUNA WAMWALIRA. MULUNGU, THANDIZENI. ITANANI MOSE.

EKSODO 12:28

EKSODO 12:29-31

MONGA MOMWE MULUNGU ANALONJEZERA MAKOLO AO, PATATHA ZAKA 400, AISRAELI ANATULUKA MU IGUPTO. AIGUPTO ANAPEREKA KWA AHEBRI GOLIDE, ZOKONGOLETSERA, NDI CHAKUDYA, NDI CHILICHONSE CHIMENE AKANATHA KUNYAMULA PA ULENDO WAO. NTHAWI IMENEYO AHEBRI ANASANGALALA KWAMBIRI; POPEZA LINALI TSIKU LOYAMBA LA FUKO LATSOPANOLO.

AMUNA 600,000, PAMODZI NDI AKAZI NDI ANA, ANATULUKA MU IGUPTO KUPITA KU DZIKO LAMALONJEZANO.

MASANA MULUNGU ANKAWATSOGOLERA NDI MTAMBO, UMENE UNKAWAPATSA MTHUNZI, NDIPO USIKU ANKAWATSOGOLERA NDI MOTO, UMENE UNKAWAUNIKIRA.

EKSODO 12:21-22, 31-38

MUTU 4:
EKSODO

ANAYENDA MPAKA KUPYOLA MAPIRI NAKAFIKA PAFUPI NDI NYANJA YOFIIRA. KUMENEKO ANAMANGA MSASA NAMAKAMBIRANA ZA MMENE ANGAOLOKERE NYANJA YA MADZI AMBIRIYO.
ATATHA KULIRA MWANA WAKE, FARAO ANAKWIYA KWAMBIRI KUPOSA KALE. NCHIFUKWA CHIYANI ADALOLA KUTI AKAPOLO AKE AMUKE?
KONZANI MAGARETA. LONDOLANI AHEBRI. MUWAPHE ONSEWO, KAPENA MUBWERERE NAWO KUNO.
TIDZACHITA MONGA MWANENERA, MFUMU.

EKSODO 14:5-7

EKSODO 14:5-13



EKSODO 14:15-22

EKSODO 14:22-23

EKSODO 14:27-28

EKSODO 14:21–22, 30, 16:2–3, 16:7–8

EKSODO 16:14-15, 17:2-4; MASALIMO 78:24-25


MULUNGU ADALIZA MOSE ZOTI ACHITE.
BWERANI TIDZAONE MPHAMVU ZA YEHOVA. SIMUMUKHULUPIRIRA. MUMANGONYONG'ONYEKA NDI KUMANGODANDAULA.

ANAKUPATSANI MKATE, NDIPO TSOPANO AKUPATSANI MADZI KUCHOKERA M'MWALA WOUMAWU.

AAAAAAA!
EEEEEE!

EKSODO 17:5-6

MADZI ANAYENDA NGATI MTSINJE.

MTAMBO UNAYENDANSO, NDIPO AHEBRI ANALONGEZA KATUNDU WAO NKUMAULONDOLA M'CHIPULULUMO KUPITA KU PHIRI LOTCHEDWA SINAI.

KUMENEKO MOSE ANAPEMPHERA, NDIPO MULUNGU ANAYANKHULANSO NDI MOSEYO.

UWAKUMBUTSE ZIMENE NDINACHITIRA AIGUPTO, MMENE NDINAWAPULUMUTSIRA, MMENE NDINKAWADYETSERA, NDI MMENE NDINAWAPATSIRA MADZI KUCHOKERA M'MWALA.

UWAUZE KUTI AKAMVERA MALAMULO ANGA, ADZAKHALA ANTHU ANGA OPATULIKA PAKATI PA MITUNDU YONSE YA ANTHU A PA DZIKO LAPANSI. AKAMVERA, ADZAKHALA ANTHU ONDITUMIKIRA NGATI ANSEMBE.

MOSE, NDIKAMAYANKHULA NDI IWE, NDIZIBWERA MU MTAMBO WOLEMERA KUTI ANTHU ATHE KUONA, KUMVA NDI KUZINDIKIRA KUTI NDINE.

EKSODO 17:6, 19:1-6, 9

EKSODO 19:7-25

EKSODO 20:3-17

MOSE ATATSIKA PHIRILO, ANAITANA ATSOGOLERI 70 A AISRAELE NAWAUZA ZA MALAMULO KHUMI A MULUNGU.
TIDZAWATS ATIRA.
NDI MALAMULO ABWINO.
INU ANTHU 70 MUBWERERE NDI INE KU PHIRI. MULUNGU ADZAKUMANA NANU KUMENEKO MONGA ANACHITIRA NDI INE. MUKADZIONERE NOKHA, PAJA ZAKUMVA ZIMAPWETEKETSA MUTU. KOMA POYAMBA NDIYENERA KULEMBA M'BUKU MALAMULO AMENE MULUNGU ANANDIUZA.
MOSE ANAYENERA KULEMBA MOSAMALA ZONSE ZIMENE MULUNGU ANAYANKHULA. MZIMU WA MULUNGU ANAMUTHANDIZA KUTI ASAPHOPHONYEPO KANTHU.
MOSE ATATHA KULEMBA MAUWO, ANASONKHANITSA ANTHU ONSE PAMODZI NAWAWERENGERA MAU A MULUNGU AJA.
ZONSE ZIMENE MULUNGU WANENA NDI ZABWINO, NDIPO TIDZAZIMVERA.
CHONCHO FUKO LA ISRAELE LINACHITA PANGANO NDI MULUNGU. MULUNGUYO ADALONJEZA KUWADALITSA, KUWAPATSA MOYO, NDI KUWATETEZA KWA ADANI AO, NDIPO IWO ANALONJEZA KUTI ADZAMVERA MALAMULO ONSEWO, NDIPO KUTI ADZACHITA CHILUNGAMO.
MULUNGU ANALAMULA MOSE KUTI APEREKE NSEMBE YAMAGAZI NDI KUWAZA ANTHU MAGAZIWO.
ONSE ANALI OCHIMWA, OYENERA KUFA NDITHU, KUPHATIKIZAPO MOSE NDI AARONI. KOMA MULUNGU ANAWACHITIRA CHIFUNDO. ANAKONZA NJIRA YOWAPULUMUTSIRA. POPHA MWANAWANKHOSA WOSALAKWA NDI KUWAZA FUKOLO MAGAZI, MULUNGU ANAPHIMBA MACHIMO AO NDIPO SANAWAPHE NGAKHALE ANALI OYENERA KUFA. MWANAWANKHOSA AMENE SANAYENERA KUFA NDIYE ANAFA M'MALO MWA ANTHU OCHIMWA AMBIRI AMENE ANAYENERA KUFA.
TSOPANO POPEZA MACHIMO ANU AKHULULUKIDWA, INU ANTHU 70 MUPITA NDI INE PAMWAMBA PA PHIRILO NDIPO MUKAONA ULEMERERO WA MULUNGU.

EKSODO 24:1-8

EKSODO 24:9-10

EKSODO 20:4, 25:8-9, 28:1-3, 28:1-4; EZEKIELE 1:10, 10:11, 28:14

EKSODO 32:5-10

EKSODO 20:3-4, 32:15-20

EKSODO 32:26-28



EKSODO 34:28-32, 39:32; NUMERI 21:5-6

POSAKHALITSA MSASA WONSE UNADZAZA NDI NJOKA ZAULULU.
TITHANDIZE NI MULUNGU!
NJOKA ZINKAWAPEZA NGAKHALE M'MAHEMA MWAO USIKU.
SIIIIII
THANDIZENI. NDALUMIDWA.
AIIIIIII!
AI, EBENI!
AMAI!
NGAKHALE ANA ANAZUNZIKA CHIFUKWA CHA KUCHIMWA KWA MAKOLO AO.

NUMERI 21:6

MUMSASA MONSE, KULIRA KOSONYEZA KUZUNZIKA NDI KUDANDAULA KUNAMVEKA. MALIPIRO A UCHIMO NDI OWAWA KWAMBIRI.

MUMSASA MONSE ZINTHU ZAFIKA PAMENEPA NDIPO ZIPYOLABE APA. ANTHU AMBIRI AFA KALE.

TIFUNEFUNE KOMWE KULI MOSE BASI. ZIMENEZI AKUCHITA NDI MULUNGU. WAKWIYA CHIFUKWA CHA MACHIMO A ANTHUWA.

TCHAAA!

UYANKHULE NDI MULUNGU. INDE TIYENERA KULANGIDWA, KOMA UMUPEMPHE KUTI ATICHITIRE CHIFUNDO.

KODI ANTHU ADZAZINDIKIRA LITI KUTI MULUNGU AMADANA NDI TCHIMO? AYENERA KUMVERA MALAMULO AKE NDI KUKHALA ANTHU OPATULIKA.

MULUNGU, CHONDE CHITIRANI CHIFUNDO ANTHU ANU. AKHULULUKIRENI.

PITA. KAPANGE NJOKA YAMKUWA, YOFANANA NDI ZIMÉNE ZIKULUMA ANTHU. UYIIKE PAMTENGO POTI ANTHU ONSE ATHA KUYIONA. UWAUZE KUTI AZINGOYANG'ANA NJOKA YAMKUWAYO, NDIPO ADZACHIRA NTHAWI YOMWEYO.

NUMERI 21:7-8

MULUNGU WAKONZA NJIRA. MUNGOYANG'ANA NJOKA YAMKUWAYO, NDIPO MUDZACHIRITSIDWA.
AFA BASI.
A! MULUNGU WAKONZA NJIRA. TANGOTSEKULANI MASO ANUWO, YANG'ANANI. YANG'ANANI KUTI MUKHALE NDI MOYO.
NCHOZIZ WITSA!
TIYENERA TIUZEKO ANZATHU.
INE NDACHIRA. NDIUZAKONSO ENA.
YANG'ANANI KUTI MUKHALE NDI MOYO!

NUMERI 21:9

NUMERI 21:9, 32:13

MOSE, UMAGANIZA KUTI IWE WEKHA NDIYE UKHOZA KUYANDIKIRA KWA MULUNGU. IFENSO NDIFE OYERA MONGA MMENE ULILI IWEYO. ZOONA ZAKE NZAKUTI, ANTHU ONSEWA NDI OYERA. TSOPANO PALIBE OCHIMWA PAKATI PATHU, NDIPO MULUNGU AMAKHALA PAKATI PATHU. SITIKUFUNA KUTI IWEYO NDI AARONI MUZITIUZA ZOYENERA KUCHITA, SITIKUFUNANSO KUTI MUKHALE OTIWERUZA. IFENSO TIKHOZA KUMAWERUZA MONGA INU NOMWE.
AAAA, NDATOPA NDI KUMANGOYENDA M'CHIPULULU MUNO, NDIPO MULUNGU AKUNGOTIPHA PA ZIFUKWA ZOSAKWANIRA.
INDE, MOSE NDIYE ANALAKWA. KAYA AMAYEMBEZEZA KUTI TIZICHITA MOTANI?

MOSE ANAPITA M'HEMA LOPATULIKA KUKAMFUNSA MULUNGU ZOTI ACHITE.

MULUNGU AKUTI, "MUKUDZISENZETSA NOKHA MAUDINDO, INU ANA A LEVI. ZIKANAKHALA BWINO KUTI ANTHU ANU AKHALE ANSEMBE OSANKHIDWA NDI MULUNGU.
MAWA AMBUYE ADZAWERUZA PAKATI PATHU, NDIPO TIDZADZIWA KUTI ANSEMBE ENIENI A MULUNGU WOYERA NDANI, NDIPONSO KUTI ANSEMBE ABODZA NDANI. MUBWERE KU HEMA LOPATULIKA MAWA MMAWA. MUKABWERETSE ZOFUKIZIRA LUBANI NDI MOTO MMENEMO.

NUMERI 16:2-6

NUMERI 16:19-24

NUMERI 16:28-33

TENGANI ZOFUKIZIRA LUBANI ZAO ZAMKUWA NDIPO MUZIGWIRITSE NTCHITO POPANGIRA CHOTCHINGIRA GUWA LA NSEMBE.

MUKADZAONA CHOTCHINGIRA GUWA CHAMKUWA MUZIDZAKUMBUKIRA TSIKU LIMENELI, PAMENE ANTHU ANANYOZERA MALAMULO A MULUNGU NAFUNA KUDZIIKA PA UDINDO WA UNSEMBE.

ANA A ISRAELE SAKANAIWALA TSIKU LIMENELO. MULUNGU ANAONETSA KUTI MOSE NDIYE ANALI MNENERI WAKE, NDIPO OKHAWO AMENE IYE WASANKHA NDIWO ANKAYENERA KUKHALA ANSEMBE.

ULEMERERO WA MULUNGU UNKAKHALA PA HEMA LOPATULIKALO NTHAWI ZONSE NDIPO AISRAELE ANKATSATIRA MOSE KULIKONSE M'CHIPULULU MUJA KWA ZAKA 40.

ULEMERERO WA MULUNGU ULI NAFE NDIPO AKUTIPATSA MKATE KUCHOKERA KUMWAMBA.

MULUNGU ANKAWAGWETSERABE MKATE KUCHOKERA KUMWAMBA NDIPO ANKAWAPATSA MADZI KUCHOKERA M'MWALA. MOTO UNKAWAKUTA USIKU NDIPO MTAMBO UNKAWAKUTA USANA. ANAKHAZIKIKA NDIPO ANAPHUNZIRA KUSUNGA MALAMULO A MULUNGU.

NUMERI 16:37-38

PAFUPIFUPI 1451 B.C. – DEUTERONOMO 34:4-5

PANAPITA PAFUPIFUPI ZAKA 500 KUCHOKERA PAMENE MULUNGU ADAALIZA ABRAHAMU KUTI ACHOKE M'DZIKO LA KWAO NDI KUPITA KU DZIKO LIMENE MULUNGU ADZAMPATSE.
LONJEZO LA MULUNGU KWA ABRAHAMU NDI SARA, LOTI ADZAKHALA MTUNDU WAUKULU KUPYOLERA MWA ISAKE, LINAKWANIRITSIDWA. ANA 12 A YAKOBO, AMENE DZINA LAKE LINASINTHIDWA KUKHALA ISRAELE, ANALI MAFUKO 12 NDIPODI UNALI MTUNDU WAUKULU WA ANTHU.
ANACHOKERA KU UKAPOLO, ANAYENDA M'CHIPULULU NDI MOSE, ANALANDIRA MALAMULO A MULUNGU, NDIPO TSOPANO ANALI PAFUPI KULOWA M'DZIKO LAMALONJEZANO. PA ULENDO WONSE WA M'CHIPULULU, MNYAMATA WINA ANKAKHALA NDI MOSE NTHAWI ZONSE, AMAONA NDI KUPHUNZIRA ZA KAYENDETSEDWE KA MTUNDU WA ISRAELE.
MNYAMATA AMENEYO ATAKULA, ANAKHALA MSILIKALI WAMPHAMVU KWAMBIRI; DZINA LAKE NDILO YOSWA.

DEUTERONOMO 34:9; YOSWA 5:12

MUTU 5:
ANENERI

DEUTERONOMO 18:9-11

ANTHU OPEMBEDZA MAFANO A M'DZIKO LAMALONJEZANO SANKAFUNA AISRAELE M'DZIKOMO NDIPO ANKACHITA NAWO NKHONDO POFUNA KUSUNGA DZIKO LAO. KOMA MULUNGU ADAAPATSA MPHAMVU ANA A ISRAELE KUTI AGONJETSE ADANI AOWO.
WABWERA BWANJI M'KACHISI WOPATULIKA UNO?
MWAPHA MWANA WANU WOMALIZA.
ITATHA NKHONDO YOOPSAYO, AHEBRI ANAPAMBANA ADANI AO, NDIPO DZIKOLO LINAKHALA M'MANJA MWAO. YOSWA ANAYANKHULA NDI AISRAELEWO.
GOGO WATHU, ABRAHAMU ANACHOKERA PAKATI PA ANTHU OPEMBEDZA MAFANO. MULUNGU ANAYANKHULA NAYE NDIPO ANAMULONJEZA KUTI ADZAMSANDUTSA MTUNDU WAUKULU.
.// MULUNGU ANANENANSO KUTI ANTHU AKE ADZAPITA KU IGUPTO KUMENE AKAKHALEKO ZAKA 400, PAMBUYO PAKE ADZAWATULUTSA NDI KUWABWEZERA KU DZIKO LINO LIMENE INU MUKUKHALAMO TSOPANO. TAONANI, KWA ZAKA ZOPITIRIRA 500, MULUNGU WASUNGA MALONJEZANO AKE KWA ABRAHAMU.
// TSOPANO PITANI NDI KUKAKHALA PALIPONSE M'DZIKO LINO. MUSATENGERE MAKHALIDWE A ANTHUOCHIMWA AMENE ANKAKHALA M'DZIKO LINO INU MUSANABWEREMO, CHIFUKWAMULUNGUADZAKUWERUZANI MONGA WAWERUZIRA IWOWO.

YOSWA 24:2-14

M'DZIKO LATSOPANOLO ANALI PA MTENDERE. ALIYENSE ANALI NDI MUNDA WAKE NDIPO ANALI NDI CHAKUDYA CHAMBIRI. MULUNGU ANAWADALITSA KUPOSA ANTHU ENA ONSE.

CHAKUDYA CHANU CHAKONZE DWA.

TIKANGOTENGA ICHOCHO MUTSEKE

MONGA MOMWE MULUNGU ANALONJEZERA, AHEBRI ANACHULUKANA KWAMBIRI MPAKA ANADZAZA DZIKOLO. MIZINDA YAO INKACHITA BWINO CHIFUKWA CHOFUNIRANA ZABWINO NDI CHILUNGAMO. DZIKO LATSOPANOLO LINKATCHEDWA ISRAELE.

MTENDERE UKHALE NAWE, MLONGO WANGA. KODI NSOMBAZI ZILI BWINOBWINO?

ZILI BWINOBWINO MONGA MWA NTHAWI ZONSE POPEZA ZIKUNGOCHOKERA KU NYANJA KUMENE.

EKSODO 21:28-29; YOSWA 24:15-24

OWERUZA 3:7–8, 12–13, 4:1–2, 10:6–7

ANTHU A MULUNGUWO AKAONA CHILANGO, ANKAKUMBUKIRA MALAMULO AKE NDI KUVOMEREZA MACHIMO AO.
O YEHOVA, TIKHULULUKIRENI MACHIMO ATHU NDI KUTIBWEZERA MTENDERE WATHU.
AKAVOMEREZA MACHIMO AO, ANKAWAKHULULUKIRA NDI KUWABWEZERA DZIKO LAO.


ANTHU AJA ANATOPA NDI OWERUZA CHIFUKWA CHA ZOCHITA ZAO NDIPO ANAGANIZA ZOKHALA NDI MFUMU KUTI NDIYO IZIWALAMULIRA.
MNENERI AMENENSO ANALI OWERUZA, DZINA LAKE SAMUELE, ANAWACHENJEZA KUTI AKAFUNA KUKHALA NDI MFUMU NDIYE KUTI AKUKANA MULUNGU AMENE AMAWALAMULIRA, KOMA ANTHUWO SANKAFUNA KUYENDA M'CHIKHULUPIRIRO. MFUMU SAULI ANAWACHITIRA ZACHABE, ANAWALANDA NDALAMA, CHUMA CHAO, NDIPO ANA AO AAMUNA ANAWASANDUTSA AKAPOLO, ANA AO AAKAZI ANAWACHITIRA ZAMANYAZI.
TIDZALANDA MINDA YANU KUTI UFUMU UZIYENDA BWINO. SIYANI MWANA WANU KUNO. TIDZAMUSAMALIRA.



1 SAMUELE 18:10–11, 31:4, 16:1–13; MASALIMO 23:1–3

2 SAMUELE 2:4; MASALIMO 1; MACHITIDWE 13:22-23

MULUNGU ANKAYANKHULA NDI DAVIDE NDIPO ANAMUULIRA ZINSINSI ZAMBIRI ZONENA ZA M'TSOGOLO. DAVIDE ANALEMBA MAVUMBULUTSOWO M'BUKU LA MASALIMO. AMBIRI MWA MAVUMBULUTSOWO AKWANIRITSIDWA KALE.

PA ZA MPULUMUTSI WODZABWERAYO, DAVIDE ADALEMBA KUTI:

MFUMUYO IDZAWERUZA ANTHU ANU MOLUNGAMA, NDIPONSO ANTHU ANU OSAUKA MOSAKONDERA. IDZATETEZA ANTHU OSAUKA, IDZAPULUMUTSA ANTHU OSOWA, KOMA IDZAONONGA ANTHU OZUNZA ANZAO. PA MASIKU AKE CHILUNGAMO CHIDZAKULA, MTENDERE UDZACHULUKA MPAKA MWEZI UTALEKA KUWALA! IDZAKHALA IKULAMULIRA KUCHOKERA KU NYANJA INA MPAKA KU NYANJA INA, KUCHOKERANSO KU MTSINJE MPAKA KU MATHERO A DZIKO. MAFUMU ONSE ADZAIGWADIRA NDIPO MITUNDU YONSE YA ANTHU IDZAITUMIKIRA. IDZAOMBOLA MOYO WAO KWA ANTHU OWAPSINJA NDI KWA OWACHITA ZANKHANZA: IKHALE NDI MOYO WAUTALI. ANTHU AIPEMPHERERE NTHAWI ZONSE; AIPEMPHERERE MADALITSO KOSALEKEZA. DZINA LAKE LISAIWALIKE KONSE: MBIRI YAKE IKHALEPOBE MONGA MOMWE LIMAKHALIRA DZUWA. ANTHU ALANDIRE MADALITSO CHIFUKWA CHA IYO, ANTHU A MITUNDU YONSE AITCHE YODALA.

(MASALIMO 72)

MULUNGU ANATI KWA DAVIDE: UKADZAFA, NDIDZAKHAZIKITSA UFUMU WAKO MWA MWANA WAKO WAMWAMUNA. ADZAMANGA KACHISI AMENE AZIDZANDIPEMBEDZERAMO, NDIPO INE NDIDZAKHAZIKITSA UFUMU WAKE MPAKA KALEKALE.

DAVIDE ATAFA, SOLOMO ANALOWA UFUMU M'MALO MWAKE (971 B.C.). MONGA MMENE MULUNGU ADANENERA KWA DAVIDE, SOLOMO ANAMANGA KACHISI (966 B.C.) KULOWA M'MALO MWA CHIHEMA CHAKALEKALE CHIMENE CHINKAGWIRITSIDWA NTCHITO M'CHIPULULU. AISRAELE ANATUKUKA KUPOSA KALE. ZOONADI, MULUNGU ANAKWANIRITSA MALONJEZO AKE KUTI ADZAWALOWETSA M'DZIKOMO NDI KUWADALITSA.

KOMA PANALI LONJEZO LIMODZI LIMENE MULUNGU ANALI ASAKWANIRITSEBE – KUBWERA KWA MPULUMUTSI AMENE ATI ADZAONONGE NTCHITO ZA SATANA. ANTHU ANKACHIMWABE NDIPO MAGAZI A NYAMA ANKAPEREKEDWA CHIFUKWA CHA MACHIMO AO. KOMABE ANKAYAMIKA CHIFUKWA MULUNGU ADAKONZA NJIRA YOKHULULUKIRA MACHIMO AO KUFIKIRA PAMENE MPULUMUTSI ADZABWERE KUDZACHOTSERATU MACHIMO ONSE.

2 SAMUELE 7:12–16; MASALIMO 72:1–20

1 MAFUMU 12:20, 28:29; MASALIMO 2:7, 12, 22:6, 14-18, 40:8, 78:2, 45:6-7, 89:26-27, 110:1, 4, 132:11

1 MAFUMU 12:28, 13:1–2; YEREMIYA 44:17–25

1 MAFUMU 13:2-6

1 MAFUMU 13:5, 7-9

1 MAFUMU 13:10–22

MNENERI UJA ANABWERERA MWANKHAWA, PODZIWA KUTI MULUNGU AMACHITA ZIMENE WANENA. ANADZIWA KUTI AFA. KOMA SANKAYEMBEKEZA KUTI AFA POSACHEDWA, KOMANSO KUTI AFA BWANJI.

EEEEIIIII!

AMENEYU NDI MNENERI WOCHOKERA KU YUDA!

NCHODABWITSANSO KUTI MKANGOWO NDI BULU ZAKHALIRA PAMODZI PAMENEPO NGATI KUTI ZIKULONDERA MTEMBOWO.

SINDINAONEPO ZOTEREZI. MKANGO WAMUPHA KOMA MKANGOWO WANGOKHALA POMWEPO OSAFUNA KUDYA MTEMBO WAKE.

MNENERI WONAMA UJA ANATENGA MUNTHU WA MULUNGU UJA NDIPO ANAKAMUIKA M'MANDA MWAKE PAMODZI NDI ANENERI A BAALA, PAFUPI NDI PAMALO PAMENE MULUNGU ANAONONGA GUWA LA NSEMBE.

MULUNGU ADAMUKANTHA CHIFUKWA CHA KUSAMVERA KWAKE. ZOONA ZAKE NZAKUTI ZONSE ZIMENE MULUNGUYO ANANENA ZIDZACHITIKADI.

MUNTHU WA MULUNGU UJA ANAIKIDWA M'MANDA, NDIPO POSAKHALITSA AMBIRI ANAMUIWALA. GUWA LANSEMBE LIJA ANALIKONZANSO NDIPO KWA ZAKA PAFUPIFUPI 300 ANTHU OPEMBEDZA BAALA ANKAPEMBEDZERAPO, KOMA PALIBE AMENE ANATENTHA MAFUPA AO PA GUWA LA NSEMBLE LIJA MONGA ANALOSERA MUNTHU WA MULUNGU UJA.

PAMBUYO PAKE, PATATHA ZAKA 300, YOSIYA ANAKHALA MFUMU YA YUDA (640 B.C.). ANAPITA KU KACHISI NDIPO ANAPEZAKO KACHIDUTSWA KA BAIBULO. KACHIDUTSWAKO KADASAUTSA MTIMA WAKE NDIPO ANAZINDIKIRA KUTI DZIKO LINAIWALA MULUNGU WAMOYO NDI KUMATSATIRA MAFANO. CHONCHO ANALAMULA KUTI AKULUAKULU, ANSEMBE, ANENERI, NDI ONSE OKHALA MU YERUSALEMU ABWERE KUDZAMVA ZA M'BUKUMO.

ANTHUWO ANACHITA MANYAZI NDIPO ANAVOMEREZANA ZOMVERA MAU ONSE A M'BUKUMO.

1 MAFUMU 13:23-31; 2 MAFUMU 21:24, 23:1-3

2 MAFUMU 23:5, 7, 10

2 MAFUMU 23:15-16

2 MAFUMU 23:17–18, 21–22

1 MAFUMU 16:28, 31, 18:4

1 MAFUMU 17:1, 10–16

1 MAFUMU 17:17–24

1 MAFUMU 18:1- 4, 17-21

1 MAFUMU 18:22–27



1 MAFUMU 18:28-30

Aku

1 MAFUMU 18:32-34

1 MAFUMU 18:35-38

1 MAFUMU 18:38-40

1 MAFUMU 18:40-41, 44-46, 19:1

1 MAFUMU 19:1-4

1 MAFUMU 19:4, 8–12

PAMENE MPHEPO, CHIVOMEZI NDI MOTO ZINALEKA, MULUNGU ANAYANKHULA NDI ELIYA M'MAU ODEKHA, APANSIPANSI. ANAFUNSA ELIYA FUNSO LOMWE ANAMUFUNSA KALE:

ELIYA UCHITA CHIYANI KUNO?

ELIYA SADAPHUNZIRE KALIKONSE. ANKANGODZIMVERABE CHISONI, CHONCHO ANAYANKHA MONGA MOMWE ANAYANKHIRA POYAMBA:

PALIBE AMENE AKUSAMALA MALAMULO ANU KUPATULA INE NDEKHA. ANENERI ANU ONSE APHEDWA. AMENE WATSALA WOTI NKUKUPEMBEDZANI NDINE NDEKHA, NDIPO AKUFUNAFUNANSO MOYO WANGA.

CHABWINO, BWANJI TITERE: UPITE UKADZOZE ELISA KUTI AKHALE MNENERI WANGA M'MALO MWAKO.

NGAKHALE SUKUDZIWA, MULI ANTHU 7000 MU ISRAELE AMENE SANAPEMBEDZEPO BAALA KAPENA KUMPSOMPSONA MAPAZI AKE. TSOPANO PITA; BANJA LONSE LA AHABU LIDZAFA.

ELIYA ADAPEZA ELISA AKULIMA NDI NG'OMBE ZAKE NDIPO ANAMUDZOZA KUTI AKHALE MNENERI.

MULUNGU AKUTI UDZAKHALA MNENERI WAKE.

NDIPEREKA NSEMBE KWA AMBUYE NG'OMBE ZANGAZI NDIPO NDIKATERO NDIKUTSATANI.

1 MAFUMU 19:12-21

EKSODO 20:17; 1 MAFUMU 21:1–7

EKSODO 20:16; 1 MAFUMU 21:10-16

1 MAFUMU 21:17-26

1 MAFUMU 21:27, 22:6-22

1 MAFUMU 22:24-30



1 MAFUMU 22:34

WOPUSA IWE! SINDIWE MNENERI WA MULUNGU. NDIWE WABODZA! AHABU WAMWALIRA MONGA MIKAYA MNENERI WA YEHOVA ANANENERA.
KOMA SIZOONA. ANTHU ONSE OKHULUPIRIKA ANAVOMEREZANA. AHABU ANAYENERA KUPAMBANA.
SI ONSE. OSATI MIKAYA AMENE UDAMUMENYA NDI KUMUIKA M'NDENDE. ANTHU AKAMVA ZIMENEZI ALALIRA MUTU WAKO.
UKHOZA KUPITA. AHABU WAMWALIRA.
INDE NDIKUDZIWA, NDIPO MOSAKAIKA KONSE AGALU ANYAMBITA MAGAZI AKE MONGA MOMWE MULUNGU ADANENERA. AMENE ATSATIRE NDI YEZEBELI NDI ABALE AKE ONSE A AHABU. MULUNGU WAYANKHULA.
NDIBISALE
AI INU! MIKAYA ADATI NDIDZADZIWA AMENE ALI NDI MZIMU WA MULUNGU PA TSIKU LIMENE NDIDZABISALA M'KACHIPINDA KAKANG'ONO M'KATI MWA CHIPINDA CHACHIKULU.
ANA AAMUNA A AHABU ANKALAMULIRA M'MALO MWAKE, ZAKA 12 ZINAPITA YEZEBELI ALI MFUMUKAZI NDITHU. ISRAELE ANAPITIRIRA KUPEMBEDZA MILUNGU YONAMA NDIPO ANKAPHWANYA MALAMULO A MULUNGU.
MULUNGU ADAYANKHULA MOTSUTSANA NDI BANJA LA AHABU, NATI, "NTHAWI YAKWANA. ONSE A M'BANJA LA AHABU AONONGEDWA, NGAKHALE MAKANDA AMENE. PALIBE AMENE ADZASIYIDWA WAMOYO. YEZEBELI ADZADYEDWA NDI AGALU, NDIPO PALIBE AMENE ADZAMULIRE KAPENA KUMUIKA M'MANDA."
ZAKA 12 ZITAPITA.
NDIPHODE NKHOPE YANGAYI, KUTI NDIKOPE MTIMA YEHU MKULU WA ANKHONDO AKAMABWERA KUCHOKERA KU NKHONDO.

2 MAFUMU 9:30

1 MAFUMU 22:37–38; 2 MAFUMU 9:8–10

2 MAFUMU 9:32-33

2 MAFUMU 9:33-37

PAMENE ELIYA ANKAPEMPHERA, ANENERI ACHINYAMATA ANAFIKA KWA ELISA NDI UTHENGA.
MULUNGU WAYANKHULA NDI ENA MWA ANENERI ACHINYAMATA. KODI UKUDZIWA KUTI LERO LINO ELIYA MBUYE WAKO ATENGEDWA KUPITA KUMWAMBA?
INDE, WANDIUZA, KOMA KHALANI CHETE; MUSANENENSO ZIMENEZI.
ELISA, BAKHALA PANO. INE NDIKUPITA KU YERIKO.
PALI MULUNGU WAMOYO, SINDIKUSIYANI. NDIPITA NANU KULIKONSE.
KODI UKUDZIWA KUTI ELIYA MBUYE WAKO ATENGEDWA KUPITA KUMWAMBA LERO LINO?
INDE, NDIKUDZIWA. TSOPANO MUSATITOPETSE. MUNGOZISUNGA MUMTIMA MWANU ZIMENEZI. SINDILOLA KUTI ANDISIYE.
BAKHALA MU YERIKO MUNO. INE NDIKUTALIKIRA PANG'ONO, NDIKUPITA KU MTSINJE WA YORDANO.
PALI MULUNGU WAMOYO, NDI PALI INU NOMWE, SINDIKUSIYANI.
TAONA, ANENERI ACHINYAMATA AJA, AKUTILONDOLANSO.
TIWOLOKA BWANJI MTSINJEWU? ULI NDI MADZI AMBIRI LERO.
POUMA.

2 MAFUMU 2:3-7

2 MAFUMU 2:8–11

2 MAFUMU 2:11-13

2 MAFUMU 2:14-16

MUTU 6:
UNENERI WOKHUDZA KHRISTU



YESAYA 1:2-4, 7, 16, 20, 39:7; YEREMIYA 21:8-10



MULUNGU ANAYANKHULA MWA AMOSI KUTI, "NDIPO INE NDEMWE NDIDZALIMBANA NAWE NDI DZANJA LANGA LOTAMBASUKA NDI LAMPHAMVU, NDIDZAKWIYA NDIPONSO NDIDZAKALIPA KWAMBIRI. NDIDZAPHA OKHALA MUMZINDA MUNO, ANTHU NDI NYAMA ZOMWE: ADZAFA NDI MLIRI WOOPSA KWAMBIRI. NDIPO PAMBUYO PAKE, AKUTERO AMBUYE, NDIDZAPEREKA ZEDEKIYA MFUMU YA YUDA, NDI ANTCHITO AKE, ANTHU ENA, NDI ONSE OPULUMUKA KU MLIRI, KU LUPANGA, NDI KU NJALA, M'MANJA MWA NEBUKADINEZARA MFUMU YA KU BABULO, NDI M'MANJA MWA ADANI AO, NDI M'MANJA MWA ONSE AMENE AMAFUNAFUNA MOYO WAO: NDIPO ADZAWAKANTHA NDI LUPANGA; SADZASIYA NDI MMODZI YEMWE WAMOYO, KAPENA KUWAMVERA CHIFUNDO, PENA CHISONI. MKWIYO WANGA UDZAYAKA NGATI MOTO NDIPO PALIBE AMENE ADZAUZIMITSA. ADZAKUGWIRANI UKAPOLO KUPITA NANU KU BABULO, NDIPO ADZAKUPHANI NDI LUPANGA. AMBIRI MWA OPITA KU BABULO ADZAFA NDIPO ADZAIKIDWA KOMWEKO." AMOSI ANALI MNENERI PA NTHAWI YA ULAMULIRO WA UZIYA NDI YEROBOWAMU WACHIWIRI (PAFUPIFUPI 765-750 B.C.).

YEREMIYA 21:5-10; AMOSI 1:4-7


MULUNGU ANAYANKHULA MWA AMOSI, "AKAZI ANU ALI NGATI NG'OMBE ZAZIKAZI AMENE AMAFUNA KUTI AMUNA AO AZIWASAMALIRA BWINO KUTI AZIWAPATSA MKAKA. SIMUDZALAMULIRANSO AMUNA ANU. ADZAKUCHOTSANI M'DZIKO MWANU POKUKOLANI NDI MBEDZA KUTI MUKAKHALE AKAPOLO KU BABULO."
"MUDZAGONA PABWINO KWAMBIRI, MUDZADYA ZAKUDYA ZOFEWA, ZAMAFUTA. MUZIDZAMVETSERA NYIMBO UKU MUKUMWA VINYO WAMBIRI. MWATAYIRA M'FUMBI CHILUNGAMO CHANU, MWAPONDEREZA AUMPHAWI, MWAZUNZA OLUNGAMA NDIPO MWALANDIRA ZIPHUPHU, OSAUKA MWAWAMANA CHILUNGAMO. MUDZALIMA MINDA YAMPHESA, KOMA ADANI ANU NDIWO AMENE ADZAMWE VINYO WAKE. ANKHONDO ANU ADZAPHEDWA NDIPO ADZAKUGWIRANI UKAPOLO NDI KUPITA NANU KU DZIKO LACHILENDO."
MULUNGU AKUTI, "NDIDZAONONGA MAGUWA A KU BETELI NDIPO NDIDZAGWETSA NYUMBA ZANU ZIMENE MUMAGWIRITSA NTCHITO PA NTHAWI YOZIZIRA, KOMANSO NYUMBA ZIMENE MUMAGWIRITSA NTCHITO PA NTHAWI YOTENTHA. MUMAPONDEREZA OSAUKA, MUMALANDIRA ZIPHUPHU, NDIPO MUMATHUDZULA AUMPHAWI. NDAGWIRA MVULA KUTI ISAGWE, NDATUMIZA NJALA NDI MATENDA KOMA CHONSECHO SIMUKULAPA. MUMALIMA MINDA YAMPHESA YAMBIRI KUTI MUPEZE VINYO WOCHULUKA, KOMA SIMUDZAMWA VINYOYO."
AMAMA, INE NDILI NDI NJALA.

AMOSI 4-6

YESAYA 10:21, 35, 51:11 (627–586 B.C.); YEREMIYA 30:11; EZEKIELE 17:21; YOWELI 3:2; HOSEYA 13:16, 14:1–6

YEREMIYA 25:11-12; MIKA 3:12, 4:1-7 (750-686 B.C.)

YEREMIYA 34:3, 51:60-61, 52:11 (627-586 B.C.); YOWELI 3:20-21; AMOSI 9:11-15; EZEKIELE 12:15-16

EZEKIELE MUTU 25, 26:15-19, 29:12-16, 30:1-8; YEREMIYA 25:15-26; AMOS 1

DANIELE 1:2-7, 17-21, 2:1-11

DANIELE 2:12-30

DANIELE 2:31-33; 39-43

MLALIKI 12:13-14; YESAYA 9:6-7, 45:1; DANIELE 2:34-35, 44-48; 5:1-29; CHIVUMBULUTSO 20:11-21:5



DANIELE 9:1–2; YEREMIYA 25:11–12, 29:10

DANIELE ANAKALAMBA KWAMBIRI, CHONCHO SANABWERERE NAWO ANZAKE AJA. KOMABE ANKAGWIRA NTCHITO YOTAMANDIKA YOLANGIZA MAFUMU A AMEDI NDI PERISIYA, AMENE ANKAKHALA MU MZINDA WA BABULO PA NTHAWI IMENEYO. MULUNGU ADAMPATSA MASOMPHENYA AMBIRI A ZAKUTSOGOLO, MPAKA MASOMPHENYA ONENA ZA KUTHA KWA NTHAWI YA PANSI PANO. PA MALOTO AKE ENA ANAONA CHILOMBO CHA CHACHITSULO. MNGELO ADAMUUZA TANTHAUZO LA CHILOMBOCHO.

MULUNGU AKUKUONETSA ZIMENE ZIDZACHITIKA PA MASIKU OMALIZA. ADAULULA KWA NEBUKADINEZARA KUTI PADZAKHALA MAUFUMU ANAI. TSOPANO PAONEKA KALE MAUFUMU AWIRI. UFUMU UWU WA AMEDI NDI APERISIYA UKADZATHA, AGRIKI ADZABWERA. UFUMUWO UDZAGONJETSA MWAMPHAMVU KOMA SUDZAKHALITSA CHIFUKWA UDZAGAWIKA PANAI, NDIPO A MU UFUMUWO AZIDZAMENYANA OKHAOKHA MPAKA PADZATSALA MAUFUMU AWIRI OKHA. MAUFUMU AWIRIWO ADZAGONJETSA MAIKO MOLAPITSA KWA ZAKA ZAMBIRI MPAKA PAMENE ADZAGONJETSEDWE NDI UFUMU WACHINAI, NDIPO CHILOMBO CHACHITSULOCHO CHIKUIMIRA UFUMU WACHINAIWU.

UFUMU WACHINAI UDZAKHALA NGATI CHITSULO, WAMPHAMVU NDI WOOPSA KWAMBIRI KUPOSA MAUFUMU A M'MBUYOMO. UDZAGONJETSA ONSE, KOMA PA MASIKU OMALIZA UFUMUWU UDZAGAWIKA PAKHUMI. TSONO PADZABWERA MUNTHU AMENE AZIDZAYANKHULA ZA MTENDERE. IYEYU NDIYE NYANGA YOMALIZA YOMERA PAMUTU PA CHILOMBO. PA MASIKU OMALIZA, IYEYO ADZANYENGERERA ANTHU NDIPO AZIDZALONJEZA MTENDERE, KOMA M'MALO MWAKE AZIDZANGOGONJETSA ANTHUWO NDI KUWAONONGA. ADZAIKA ZINTHU ZONYANSA M'MALO OYERA, M'KACHISI WA AYUDA, KUTI KACHISIYO AKHALE ODETSEDWA MONGA MWA MIYAMBO YA AYUDA, KUTI TSONO ALEKE KUPEREKERAMO NSEMBE. NDIYENO PADZAFIKA NTHAWI YA MASAUTSO AAKULU PA DZIKO LONSE LAPANSI, KOMA OLUNGAMA ADZAOMBOLEDWA.

DANIELE 7:17-28; MATEYU 24:4-25

DANIELE, MULUNGU AFUNA KUKUONETSA ZIMENE ZIDZACHITIKA NDI NTHAWI YAKE IMENE ZIDZACHITIKIRE. KUCHOKERA PA NTHAWI IMENE LAMULO LOTI ANTHU ABWERERE NDI KUKAMANGANSO KACHISI LAPEREKEDWA, PADZAPITA ZAKA 483, NDIPO PAMBUYO PAKE MESIYA ADZAPHEDWA POLIPIRA MACHIMO A ANTHU ONSE, NDIPO KENAKA KACHISI ADZAONONGEDWANSO.

UNENERI UWU UDZAKWANIRITSIDWA, NDIPO MESIYA ADZADZOZEDWA. MACHIMO ADZAKHULULUKIDWA, NDIPO ANTHU ADZAPATSIDWA KULUNGAMA KOSATHA.

MONGA MOMWE DANIELE ADALEMBERA, MESIYA ADALOWA MOPAMBANA MU YERUSALEMU PA TSIKU LOMWE ZAKA 483 ZIMATHA.



MULUNGU ADAUZA ADAMU NDI HAVA KUTI MBEU YA MKAZI IDZABWERA KUDZAONONGA WOIPAYO. ADAUZA NOWA KUTI MESIYA ADZABWERA KUCHOKERA M'BANJA LA SEMU, OSATI YAFETE KAPENA HAMU. MULUNGU ADAUZA ABRAHAMU KUTI MPULUMUTSI ADZACHOKERA MWA ZIDZUKULU ZAKE KUPYOLERA MWA ISAKE MWANA WAKE. MULUNGU ADAUZA ISAKE KUTI WOLONJEZEDWAYO ADZACHOKERA MWA YAKOBO MWANA WAKE, NDIPO ADAUZA YAKOBO KUTI KHRISTU ADZACHOKERA MWA YUDA.

MULUNGU ANAPEREKA KWA ANENERI MAUNENERI AMBIRI ACHINDUNJI ONENA ZA MOYO WA MPULUMUTSI WOLONJEZEDWAYO. AMATI NGWACHIKHALIRE, KUTI ADZABADWA MWA NAMWALI MU MZINDA WA BETELEHEMU WA YUDA, ADZAKHALA WODZICHEPETSA M'MAKHALIDWE AKE, NDIPO ADZAKHALA WOFATSA NDI WOKWERA PA BULU. AMBUYE ADZAIKA MZIMU WAKE PA IYE, NDIPO ADZAWERUZA ANTHU A MITUNDU INA. ADZAKHALA KUWALA KWA ANTHU A MITUNDU INA NDIPO ADZABWERETSA CHIPULUMUTSO KWA ANTHU ONSE A PA DZIKO LAPANSI. ADZAKHALA MESIYA WOZUNZIKA NDIPO ANTHU AKE ADZAMUKANA, NDIPONSO ADZAFA POKHOMEDWA MANJA NDI MAPAZI AKE. ADZAMUKWEZA PA MTANDA ALI WAMALISECHE NDIPO ADZAMVA LUDZU, KOMA M'MALO MWAKE ADZAMPATSA VINYO WOSASA KUTI AMWE. ADZAFERA PAKATI PA MBAVA NDIPO ADZAIKIDWA M'MANDA A MUNTHU WOLEMERA.

GENESIS 49:9-10; SALIMO 22, 53; YESAYA 7, 9:1-2, 42:1, 49:6, 53; DANIELE 9:25-26; MIKA 5:2; ZEKARIYA 9:9; MATEYU 24:1-2; AHEBRI 2:9

MAULOSI A DANIELE OKHUDZA MAUFUMU ANAI ANAKWANIRITSIDWA MONGA MOMWE ADALOSERA. M'CHAKA CHA 330 B.C. ALEKSANDRO WAMKULU, WOCHOKERA KU GRISI, ANAYAMBA KUONETSA MPHAMVU ZAKE KWA ZAKA 7, NDIPO ANAGONJETSA MAIKO AMBIRI, KUPHATIKIZAPO UFUMU WA AMEDI NDI APERISIYA. GRISI ANAKHALA WAMPHAMVU MPAKA PAFUPIFUPI CHAKA CHA 167 B.C. POMWE UFUMU WACHINAI, ROMA, ANAYAMBA KUGONJETSA MAUFUMU ENA.

PA MALOTO A NEBUKADINEZARA, ROMA ANKAIMIRA MAPAZI NDI MIYENDO YACHITSULO, NDIPO M'MASOMPHENYA A DANIELE, ROMA ANKAIMIRA CHILOMBO CHACHITSULO CHIJA, CHIMENE CHINAKUZA MPHAMVU ZAKE NDI KUGONJETSA MAIKO AMBIRI, MONGA MOMWE MNENERI ADALOSERA. M'CHAKA CHA 5 B.C., ROMA ANKALAMULIRA ISRAELE NDI DZANJA LACHITSULO.

MUTU 7: CHIPANGANO CHATSOPANO, KUBADWA KWA KHRISTU, NDI MAYESERO AKE

PATAPITA ZAKA 500

ZAKA ZOPOSA 500 ZINAPITAPO KUCHOKERA PA MAULOSI A DANIELE. M'CHAKA CHA 6 B.C. AROMA ADAPATSA AYUDA UFULU WA CHIPEMBEDZO KOMA ANKAWAKHOMETSA MSONKHO WAUKULU KWAMBIRI. KACHISI ADAAMANGIDWANSO NDIPO ANALI NGATI MTIMA WA MOYO WA AYUDA. AMBIRI ADAIWALA MAUNENERI OKHUDZA ZA KUBWERA KWA MESIYA, KOMA ENA ANKASUNGABE MALAMULO NAMAYEMBEKEZA KUBWERA KWA KHRISTU. MMODZI MWA IWO ANALI MUNTHU WINA WOKALAMBA WOTCHEDWA SIMEONI. ANALI MUNTHU WOYERA MTIMA AMENE ANKAFUNITSITSA ATAONA UJA AMENE ANENERI ADAKAMBA ZA IYE. KWA ZAKA ZAMBIRI ANKAWERENGA MAUNENERI NDIPO ADAZINDIKIRA KUTI NYENGO YA MESIYA IKUYANDIKIRA. KOMA TSOPANO ANALI WOKALAMBA NDIPO MASIKU A MOYO WAKE ANKACHEPERACHEPERA. ZAKA 4,000 ZINAPITAPO KUCHOKERA PAMENE MULUNGU ADALONJEZA HAVA KUTI MBEU YAKE IDZABWERA KUDZAONONGA NTCHITO ZA WOIPAYO.

NTHAWI INALI ITAKWANA TSOPANO. MAULOSI OPOSA 350 ANAYENERA KUKWANIRITSIDWA.

GENESIS 3:15; SALIMO 45:6; YESAYA 7:14, 9:6; DANIELE 9:25-26; MIKA 5:2; LUKA 2:25-26

PAMENE SIMEONI ANKAKALAMBIRAKALAM BIRA NAMADIKIRABE M'KACHISI, KUYEMBEKEZA KHRISTU WOLONJEZEDWAYO, WANSEMBE WINA WOTCHEDWA ZEKARIYA ADAPITA KU KACHISI KUKAPEMPHERA. IYE NDI MKAZI WAKE ANALI OKALAMBA NDIPO KUFIKIRA NTHAWI IYI ANALI ASANABEREKEPO MWANA.

LUKA 1:5-20, 26-40

ELIZABETI!
MARIYA, MWANA WANGA!
NDIWE WODALA MWA AKAZI ONSE, NDIPO NCHODALITSIKANSO CHIPATSO CHA M'MIMBA MWAKO. INE NDINE YANI KUTI MAI WA MULUNGU ABWERE KUDZANDICHEZERA? POPEZA PAMENE NDINAMVA MAU AKO, MWANA AMENE ALI M'MIMBA MWANGA ANATAKATAKA NDI CHIMWEMWE.
MOYO WANGA UKULEMEKEZA MULUNGU, NDIPO MZIMU WANGA WAKONDWERA NDI MULUNGU MPULUMUTSI WANGA. ZIKADZACHITIKA IZI, MIBADWO YONSE IDZANDITCHA WODALA, POPEZA AMBUYEYO WACHITA ZINTHU ZAMPHAMVU.
WAKWEZA ENAFE PAMENE NDIFE OCHOKERA KU MABANJA OSAUKA. MONGA ADANENERA KWA KHOLO LATHU ABRAHAMU, IYE WATIKUMBUKIRA MWA CHIFUNDO CHAKE.
MARIYA ANACHEZA NDI ELIZABETI PAFUPIFUPI MIYEZI ITATU.
NTHAWI YOTI ELIZABETI ABALE MWANA INAFIKA.
ZEKARIYA AKUTI AMENEYO ADZAKHALA MWANA WAMWAMUNA; AKUTI MNGELO NDIYE ADAMUUZA CHONCHO.
CHABWINO, AKAKHALA MWANA WAMWAMUNA NDIYESA ADZATCHEDWA ZEKARIYA POTSATA DZINA LA ATATE AKE.
NDI UYO AKUBWERA APOYO. TIMUFUNSE.
AKUTI MNGELO NDIYE ADAMUCHITITSA KUTI ASAMAYANKHULE CHIFUKWA SADAKHULUPIRIRE.
MWANAYO MUDZAMUTCHA DZINA LOTI CHIYANI?
AKUFUNA POTI ALEMBEPO.
AKUTI DZINA LAKE ADZATCHEDWA YOHANE, MONGA MOMWE MNGELO ADAMULAMULIRA.
KOMA M'BANJAMU MULIBE AMENE AMADZIWIKA NDI DZINA LOTI YOHANE
NDI MNYAMATADI, MNYAMATA WA CHEYA CHAMBIRI.
DZINA LAKE NDI YOHANE, POTSATA MAU A AMBUYE. ADZAONETSA MESIYA KWA AISRAELE, ANTHU A MTUNDU WATHU.
AKUYANKHULA! PATAPITA MIYEZI YONSEYI, TSOPANO AKUYANKHULA!
KODI TINENE KUTI AMENEYU NDI ELIYA POTSATA MAU A ANENERI?

LUKA 1:41–64

GENESIS 3:15; YESAYA 7:14, 9:7; MATEYU 1:18-23; LUKA 1:32-33

YOSEFE NDI MARIYA ANKAKHALA KU NAZARETI WA KU GALILEYA, KOMA PADALI ULOSI WAKUTI MESIYA ADZABADWIRA KU BETELEHEMU WA YUDEA (MIKA 5:2). MARIYA TSOPANO ANKAYEMBEKEZA KUBALA MWANA WAKE MU MZINDA UMENE ANENERI SANAUKAMBEPO. SANKADZIWA ZA UNENERI UMENEWU, NDIPO PANALIBENSO CHIFUKWA CHOTI APITIRE KU BETELEHEMU, KUTALI NDITHU.
TAMVERANI, TAMVERANI, IZI ZACHOKERA KWA MFUMU YA KU ROMA, ZASINDIKIZIDWA NDI KAESARA MWINI WAKE, KUDZAKHALA KALEMBERA NDIPO ANTHU ONSE APITE KU MIZINDA IMENE ADABADWIRA KUTI AKALEMBETSE KALEMBERA WA MSONKHO.
YOSEFE, NDIYE KUTI UYENERA KUPITA KU BETELEHEMU. UDZAPITA MWANA AKABADWA.
SIZIKHALA BWINO NDIKAKUSIYA WEKHA, NDIYE KUTI ANTHU ADZAYAMBA KUDABWA. NDIPTA NDI IWE BASI.
MARIYA, NDIKANADZIWA SINDIKADAKUTENGA. MWINA TINGOBWERERA.
AI, NDIYENERA KUKHALA PAFUPI NAWE KUFIKIRA PAMENE MWANAYO ADZABADWA. PALIBE AMENE AKUMVETSA ZIMENE ZINATICHITIKIRAZI.
ZINAWATENGERA PAFUPIFUPI SABATA IMODZI KUYENDA MTUNDA WA MAMAILOSI NGATI 100.
NGATI NKUTHEKA TIYENDE MWACHANGU. NDIYESA NTHAWI YAKWANA.
NDIONA NGATI TINGAPEZE CHIPINDA CHOGONA M'NYUMBA INA YA ALENDO.
MARIYA, NDAPEZA ZAMBA WOTI ATITHANDIZE.
KODI MULIBE MALO M'NYUMBA YA ALENDOYO?
AI, NDI YODZAZA.
MUNAFUNITSITSA KUTI MWANA WANU ABADWIRE PABWINO. KOMA TAONANI WABADWIRA M'KHOLA LA NG'OMBE.
MUSADANDAULE. TSIKU LINA ADZALAMULIRA DZIKO LONSE LAPANSI AMENEYU.
AI NDITHU, KWA INE, MWANAYU AKUONEKA MONGA AONEKERA ANA ENA ONSE.

LUKA 2:1–7

NCHIYANI? NDI MNGELO!
ZIKWIZIKWI ZA ANGELO!
MUSAOPE, PAKUTI MULUNGU WANDITUMA KUTI NDIDZALENGEZE UTHENGA WABWINO KWA ANTHU ONSE, PAKUTI LERO WAKUBADWIRANI MPULUMUTSI MU MZINDA WA DAVIDE, AMENENEYO NDIYE MESIYA WA AYUDA, AMBUYE.
ULEMERERO KWA MULUNGU M'MWAMBAMWAMBA! MULUNGU WABWERETSA MTENDERE PA DZIKO LAPANSI POPEZA AMAFUNIRA ZABWINO ANTHU AKE.
CHIZINDIKIRO CHAKE NDI ICHI: MUKAPEZA KHANDA LITAKULUNGIDWA M'NSALU YOIKIRA MALIRO, LITAGONA MODYERA NG'OMBE.
NZODABWITSA ZEDI! ANGELO KUONEKERA IFE!
IMANI KAYE MPAKA NDIUZE MKAZI WANGA!
KODI MWAMVA ZIMENE WANENA? MESIYA WABADWA MU ISRAELE.
NDIKUFUNA NDIPITE NDIKAONE.
MPULUMUTSI! MTENDERE KWA ANTHU! MWANA? TIYENI TIPITE TIKAMUONE!
PEPANI KUTI TIKUVUTITSANI, KOMA MNGELO ANATI TIBWERE KUNO.
MESIYA!
ANGAMVETSE IZI NDANI, MULUNGU KUSANDUKA KHANDA?

LUKA 2:8-20

NTHAWI INAFIKA KUTI MARIYA NDI YOSEFE APEREKE MWANA WAKHANDAYO KWA WANSEMBE NDI KUPEREKA NSEMBE ZOLAMULIDZWAZO POTSATA MWAMBO WA AYUDA.
YOSEFE, AKA NKOYAMBA KUTI MWANAYU AFIKE KU KACHISI, NDIPO PALIBE AMENE AKUDZIWA KUNO KUTI YESU NDI KHRISTU.
NDIPO NDIYESA KUTI TISAUZE ALIYENSE. TIYENI TIDIKIRE MPAKA AKULE.
SIMEONI ANALI M'KACHISIMO.
NDI AMENEYO. TAMUDIKIRA NTHAWI YAITALI.
MARIYA, NDANI AMENEYO?
SINDIMDZIWA. PALIBE AMENE AMATIDZIWA KUNO.
WODALITSIKA NDINU YEHOVA, INU AMBUYE MULUNGU WATHU. TSOPANO NDIKHOZA KUFA MU MTENDERE, CHIFUKWA NDAONA CHIPULUMUTSO CHANU, MONGA MOMWE MUNALONJEZERA. ADZAKHALA KUWALA KWA ANTHU A MITUNDU INA NDI ULEMERERO KWA ISRAELE.
KOMA, MWAZINDIKIRA BWANJI?
MVERENI, MWANA UYU ADZACHITITSA KUTI AMBIRI MU ISRAELE ADZUKE NDI KUTI ENA AGWE, NDIPO ADZAMTSUTSA NDI KUDANA NAYE.
INDE, NDIPO MTIMA WANU UDZASWEKA POONA ZIMENE ZIDZAMCHITIKIRA.
TAONANI! MESIYA. WAFIKA KU KACHISI WAKE. UYU NDIYE AMENE ANENERI ADANENA ZA IYE.
AMENEYO DZINA LAKE NDI ANA. MOYO WAKE WONSE WAKHALA AKUDIKIRA MESIYA.
MNYAMATA IWE, MWANA UYU NDI KHRISTU, MPULUMUTSI WA DZIKO LONSE LAPANSI. ADZAPULUMUTSA AISRAELE KU MACHIMO AO.
KUCHOKERA NTHAWI IMENEYO, ANA ANKANENA ZA IYE KWA ONSE OFUNA CHIPULUMUTSO.

LUKA 2:27–38

MATEYU 2:1–8; MIKA 5:2

ZINALI ZOCHITITSA CHIDWI NDITHU MMENE ALEMBI AJA ANADZIWIRA MALO ENIENI KUMENE MWANAYO ADZABADWIRA. KOMABE SANKAKHULUPIRIRA ANENERI AOWO.
ZOLEMBA ZA ANENERI A KU ISRAELE NDI ZOPAMBANA ZEDI. SINDINAONEPO ZOLEMBEDWA ZACHINDUNJI CHONCHI.
TAONANI! NYENYEZI YOMWE TIDAONA KUMMAWA KUJA!
KOMA IKUONEKA NGATI SINYENYEZI YOMWE TIDAIONAYO. SIKUYENDA NDI NYENYEZI ZINA, NDIPO NDI YOWALA KWAMBIRI.
MUONETSETSE PAMENE ILILIPO, NDIPO MAWA TIDZAITSATA.
ONANI, YAIMA PAMWAMBA PA NYUMBA. KOMA KUNO SI KU BETELEHEMU. PAPITA MIYEZI YAMBIRI. MWINA MWAKE ADACHOKAKO.
TAYENDA ULENDO WAUTALI KWAMBIRI, NDIPO TAKHALA PANG'ONO KUFIKA KUMENEKO.
ZOONADI NDI NYENYEZI YODABWITSA. KOMA ILI PAFUPI ZEDI.
SITIKUFUNA TIKUSOKONEZENI, KOMA TAYENDA ULENDO WA MASABATA AMBIRIMBIRI POFUNA KUDZAONA NDI KUPEMBEDZA MFUMU IMENE YANGOBADWAYI.
MUNADZIW A BWANJI?
TIMAWERENGA MALEMBO OYERA A ANTHU ONSE. ANENERI ANU ADALOSA ZA KUBWERA KWAKE, NDIPO NYENYEZI INAONEKA KUTI ITITSOGOLERE. NGAKHALE TSOPANO YAIMA PAMWAMBA PA NYUMBA YANUYI.
MODZICHEPETSA TIKUPEREKA MPHATSO ZOCHEPAZI POLEMEKEZA MPULUMUTSI WA DZIKO LONSE LAPANSI. ADZATEMBENUZIRA ANTHU AMBIRI KU CHILUNGAMO.
USIKU UMENEWO, MULUNGU ADAYANKHULA ANZERUWO M'MALOTO NDIPO ADAWAUZA KUTI ASADZIWITSE HERODE KUMENE KULI MWANAYO, KOMA KUTI ABWERERE KWAO PODZERA NJIRA INA. NDIPO MULUNGU ADAYANKHULANSO NDI YOSEFE, KUMUUZA KUTI ATHAWIRE KU IGUPTO, POPEZA HERODE AMAFUNAFUNA KUPHA MWANAYO.

MATEYU 2:9-12

YEREMIYA 31:15; HOSEA 11:1; MATEYU 2:13–23

YESAYA 9:7; LUKA 2:42-46; 2 TIMOTEO 3:16-17

YESU, TAYANG'ANA PONSEPONSE KUFUNA IWE. WATIZUNZIRANJI CHOTERE?
WAKHALA NDI IFE MASIKU AWIRI. MULI NDI MWANA WODABWITSA.
MUMANDIYANG'ANIRA NJI? KODI SIMUDZIWA KUTI NDIYENERA KUGWIRA NTCHITO YA ATATE ANGA?
MAU OTI, 'FURABIDA' (ATATE) AMATANTHAUZA 'FAWU' (ATATE), NDI MAU AMENE YESU ANKAKONDA KUGWIRITSA NTCHITO POKAMBA ZA MULUNGU WA KUMWAMBA.
SINDINAONEPO MNYAMATA WACHICHEPERE CHONCHI WODZIWA MALEMBO OYERA KWAMBIRI.
AMATANTHAUZA CHIYANI PONENA KUTI, "NDIYENERA KUMAGWIRA NTCHITO YA ATATE ANGA? KODI AMENE AMAMFUNAFUNA AJA SI ATATE AKE?
YESU ANABWERERA NDI MAKOLO AKE NDIPO ANKAWAMVERA. ANAPITIRIZA KUGWIRA NTCHITO YA UMISIRI WA MATABWA NDIPO ANKAKULABE M'NZERU NDI MU MSINKHU.
POPEZA NTHAWI ZONSE ANKACHITA CHILUNGAMO NDI KUFUNIRA ANZAKE ZABWINO, ANKAKONDEDWA NDI ALIYENSE. ACHINYAMATA ANZAKE ANKAGWA MU UCHIMO, KOMA YESU ANKAMVERA MALAMULO ONSE A MULUNGU KUCHOKERA PANSI PA MTIMA WAKE.
MITENGO YANU NDI YABWINO KWAMBIRI, NDIPO MULIBE MMISIRI WONGA INU M'NAZARETE. NDITENGANSO ZINA ZISANU NDI CHIMODZI ZOFANANA NDI CHIMENECHI.

LUKA 2:46-52

MALAKI 3:1; LUKA 3:2–18, 7:24, 27



YESAYA 40:3; MATEYU 3:1–12; LUKA 3:15–18; YOHANE 1:19–27, 33

MATEYU 3:13–17; LUKA 3:21–22

LUKA 3:22; YOHANE 1:29-34; 1 YOHANE 2:1-2

MATEYU 4:1-3; LUKA 4:1-3; AROMA 3:23, 5:12-21; AHEBRI 4:15

SATANA ADAYESA MUNTHU WOYAMBA, ADAMU, PAKUMUUZA KUTI ADYE CHIPATSO CHOLETSEDWA. ANAYESETSA KUBWERETSA YESERO LOMWELO KWA MWANA WA MUNTHUYU AMENE ANKAMVA NJALA NDIPONSO ANAFOOKA KWAMBIRI.
LINALI YESERO LOOPSA KWA MUNTHU AMENE SANADYE CHILICHONSE KWA MASIKU 40.
ONANI, MUKHOZA KUSANDULIZA MWALA UWU KUTI UKHALE MKATE NDI KUUDYA CHIFUKWA CHA NJALA YANUYI.
AI, AI SINDITERO, PAKUTI MALEMBO AMATI MUNTHU SADZAKHALA NDI MOYO NDI MKATE WOKHA, KOMA NDI MAU ALIWONSE AMENE MULUNGU AMAYANKHULA.
NDITSATE TSONO. NDIPITA NAWE KUMALO KOMWE UNGATHE KUMVERA MULUNGU.
UTATI UDUMPHE KUCHOKERA PANO NDIPO ANGELO NKUBWERA KUDZAKUWAKHA, ANTHU ONSE ADZAONA ZIMENEZO NDIPO ADZAKULANDIRA IWE MONGA MESIYA, NDIPO NDIKUDZIWA KUTI CHIMENECHI NDI CHIMENE UNABWERERA.
UNAKAMBAPO ZA MALEMBO OYERA, NDIPO MALEMBOWO AMATI ANGELO ADZAKULANDIRA M'MANJA MWAO NDIPO ADZAKUTETEZA KUTI PHAZI LAKO LISASUMBE MWALA. TSOPANOTU IYI NDI NTHAWI YOTI UWAWONETSE MPHAMVU ZAKO.
MALEMBO AMATINSO, "USAMUYESE AMBUYE MULUNGU WAKO."
NDIKUDZIWA KUTI UMAKONDA DZIKO LAPANSI NDIPO UNABWERA KUDZALIPULUMUTSA, TSONO NDIKUONETSA CHINA CHAKE, NDIKHULUPIRIRA KUTI UDZACHIKONDA.

MATEYU 4:3-7

TAONA TSONO, KUCHOKERA PANO TIKHOZA KUONA MAIKO OTCHUKA A DZIKO LAPANSI. KODI SI A ULEMERERO WOPAMBANA? KUYAMBIRA NTHAWI IMENE ADAMU ANAGALUKIRA ULAMULIRO WAKO, MAIKOWA NDIDAWATENGA KUKHALA ANGA. ANTHU AMANDIPATSA MAIKOWA NTHAWI ZONSE. DZIKO LONSE NDI LANGA. NDINE MULUNGU WA DZIKO LAPANSILI, OSATI IWE.

KOMA NDIKHOZA KUKUPATSA LONSELI...UTATI WANDICHITIRA KANTHU KENA. UKANGOGWADA NDI KUNDIPEMBEDZA INE, NDIDZALEKERA POMWEPO KULAMULIRA DZIKOLI, NDIPO UKHOZA KULITENGA KUKHALA LAKO PAMODZI NDI ANTHU ONSE M'MENEMO. UKUTI BWANJI?

MALEMBO AMATI, "UZIPEMBEDZA YEHOVA MULUNGU NDIPO UZITUMIKIRA IYE YEKHAYO OSATI WINA AI." WALEPHERA; TSOPANO CHOKA.

SATANA ANACHOKA PAMASO PA KHRISTU. KWA NTHAWI YOYAMBA, SATANA ADAYESA MUNTHU AMENE ANALEPHERA KUMUNYENGA. YESU ANAPAMBANA MAYESO. TSOPANO DZIKO LAPANSI LINALI NDI MUNTHU MMODZI AMENE ANKAMVERA MULUNGU KOTHERATU.

MASIKU 40 AMAYESERO ANATHA, KOMA YESU ANALI WOFOOKA KWAMBIRI.

ANGELO ANAMUBWERETSERA CHAKUDYA NDI MADZI NDIPO ANAMTUMIKIRA. ATAPEZA MPHAMVU, ANAPITA KUMENE YOHANE ANKALALIKA.

MATEYU 4:8-11; LUKA 4:14

MUTU 8:
UTUMIKI WOYAMBIRIRA

YOHANE 1:35-39, 43-45, 3:30-31

YOHANE 1:45–51

YOHANE 1:40-42, 2:12-14; MARKO 3:16

YOHANE 2:15-16

MATEYU 6:5-7, 12:34; YOHANE 2:15-16; 1 TIMOTEO 6:10

MASALIMO 69:9; YOHANE 2:17–22

YESU NDI OPHUNZIRA AKE ANACHOKA KU YERUSALEMU NABWERERANSO KUMPOTO KU NAZARETE, KWAO KWA YESU.

OO, **YESU**, WABWERA KWANU. UBWERE NDI ANZAKO ONSE NDIPO NDIDZAWAKONZERA CHAKUDYA CHOKOMA.

AMAI, SITIKHALITSA KUNO – IKATHA SABATA TIZINYAMUKA.

MONGA MWA CHIZOLOWEZI CHAKE, YESU ANAPITA KU SUNAGOGE, KUMALO KUMENE AYUDA ANKAPEMBEDZERAKO PA SABATA.*

TAKONDWA KWAMBIRI POONA MMODZI WA IFE ATABWERERA KWAO NDI ABWENZI AKE. TAKHALA TIKUMVA ZODABWITSA ZA IWOWA. TIKUFUNA TIMVE ZAMBIRI BWINO LINO.

KOMA TSOPANO, YESU, KODI UNGATIWERENGEREKO MALEMBO OYERA PA TSIKU LA LERO?

YESU ANATSEKULA BUKU LA MNENERI YESAYA NAPEZA UNENERI WODZIWIKA BWINO WA MESIYA.

"MZIMU WA AMBUYE ULI PA INE, CHIFUKWA WANDIDZOZA KUTI NDILALIKE UTHENGA WABWINO KWA ANTHU OSAUKA, NDI KUPENYETSA AKHUNGU, KUMASULA OMANGIDWA, NDI KULENGEZA KUTI NTHAWI YAKWANA KUTI MULUNGU ABWERETSE CHIPULUMUTSO KWA ANTHU AKE."

LERO LINO UNENERI UWU WAKWANIRITSIDWA.

SUNAGOGE INALI NYUMBA IMENE AYUDA ANKAKUMANAMO PA SABATA KUTI APEMBEDZE MULUNGU PAMODZI. INKAGWIRITSIDWANSO NTCHITO PA ZINA ZA CHIKHALIDWE CHAO KOMANSO NGATI SUKULU. SABATA LINALI TSIKU LOMALIZA PA MLUNGU ULIWONSE, AYUDA ANKALILEMEKEZA TSIKULI NDIPO SANKAGWIRA NTCHITO ILIYONSE.

LUKA 4:16–21 *SABATA NDI TSIKU LOPEMBEDZA PA MLUNGU ULIWONSE LIMENE MULUNGU ANALIKHAZIKITSA PA TSIKU LACHISANU NDI CHIWIRI, NDIPO ADALIIKA KUKHALA LIMODZI MWA MALAMULO AKE KHUMI AJA KWA AYUDA (GENESIS 2:2–3; EKSODO 20:10).

KUCHITIRA MWANO MULUNGU!
IWE NDIWE MWANA WA MMISIRI WA MATABWA.
KHALANI CHETE. TIKUPITA.
MGENDENI KUTI AFE. AKUDZIYESA MESIYA!
YESU NDI OPHUNZIRA AKE ANAPITA KU KAPERNAO, MZINDA UMENE UNALI M'MPHEPETE MWA NYANJA YA GALILEYA, KUMENE KUNKAKHALA OPHUNZIRA AKE ENA. KUMENEKONSO ANAKALOWA M'SUNAGOGE.
NDIPO MNENERI ADATI MESIYA ADZAKHALA KUUNIKA KWA ANTHU A MITUNDU INA NDIPO ADZAMUKHULUPIRIRA. WODALA NDI MUNTHU WOYERA MTIMA, CHIFUKWA ADZAONA MULUNGU. MULUNGU SANYOZA ALIYENSE WODZA KWA IYE, KAYA MYUDA KAPENA MUNTHU WA MTUNDU WINA.
WOYERA UJA. TISIYENI.
NDIKUKUDZIWANI. NDINU WOYERA UJA WA MULUNGU.
ALI NDI ZIWANDA. MTULUTSENI.
KODI MWABWERA KUDZAONONGA ZIWANDAFE, NTHAWI YATHU ISANAFIKE? TISIYENI. TAKULAKWIRANINJI?
NDANI ANAMULOLA KUTI ALOWE MUNO! TAONANI! NDI WOOPSA.
ZIWANDA, NDIKUKULAMULANI KUTI MUTULUKE MWA MUNTHUYU NDIPO MUSADZAMUVUTITSE NSO.

LUKA 4:28-35

MARKO 1:25–28; LUKA 4:35–38

MARKO 1:30–34; LUKA 4:38–40

MATEYU 5:8, 21-22, 38-42, 43-44, 6:12; MARKO 1:34;

MATEYU 5:27-28,7:13-14, 28-29, 23:27-28; YOHANE 5:18-19, 23, 29-30, 14:6

NUMERI 21:5–9; YOHANE 3:1–14

*MUNTHU WA M'GULU LINA LACHIYUDA LIMENE LINKADZIWIKA KWAMBIRI POTSATA MIYAMBO YA AYUDA NCHOLINGA CHOONETSA KUMVERA MULUNGU.



YOHANE 3:14-18

ASAMARIYA ANKAKHALA PAKATI PA YERUSALEMU NDI GALILEYA. AYUDA SANKAYANJANA NDI ASAMARIYA MWA NJIRA INA ILIYONSE, NDIPO SANKAFUNA NGAKHALE KUDUTSA M'MIZINDA YAO, POPEZA ANKAKHULUPIRIRA KUTI ASAMARIYAWO ANALI ODETSEDWA MU MZIMU. TSIKU LINA YESU ANADABWITSA OPHUNZIRA AKE PONENA KUTI:
TIYENI, NDIYENERA KUDUTSIRA KU SAMARIYA.
NDI CHIFUNIRO CHA ATATE KUTI NDIPITE KU SAMARIYA.
AMBUYE, NDI ANTHU ODETSEDWA, MBUTUMA ZENIZENI! NDI ANTHU OSAUKA NDIPO MAKHALIDWE AO NDI ACHABECHABE.
NTHAWI YA MASANA ANAFIKA PA CHITSIME CHIMENE CHINALI KUNJA KWA MZINDA.
PITANI MUKAGULE CHAKUDYA MUMZINDAMU. NDIKUDIKIRANI PA CHITSIME POMPANO.
KODI MUTSALA NOKHANOKHA?
INDE, NDIYENERA KUGWIRA NTCHITO YA ATATE ANGA.
YESU ADATOPA, ANALI NDI LUDZU, NDIPONSO ANKAMVA NJALA. NGAKHALE SINALI NTHAWI IMENE AKAZI ANKABWERA KUCHITSIMEKO, MAI WINA WACHISAMARIYA ANABWERA KUDZATUNGA MADZI.

YOHANE 4:1–8

YOHANE 4:7–29, 40

MATEYU 14:15, 6:1-7, 19-21

MATEYU 14:19-21; LUKA 9:16-17

MATEYU 14:20-23

MATEYU 14:24-29





MATEYU 14:29-30

MATEYU 14:31–33

PAMBUYO PAKE
MASIKU APHWANDOWA KULI ANTHU AMBIRI. ANTHU AMENEWA ABWERA KUCHOKERA KU MAIKO ONSE, ENA ACHOKERA KU IGUPTO NDI KU ROMA, KUMENE NDI KUTALI KWAMBIRI.
TIYENI TIPITE KU DZIWE ILO.
NDIKUKUMBUKIRA KUTI WAKHALA KUNO KWA NTHAWI YAITALI.
KODI UFUNA UCHIRITSIDWE.
NDILIBE MUNTHU WOTI NKUNDITHANDIZA.
DZUKA, YALULA MPHASA YAKO, NDIPO YENDA.
NDINU YESU, SICHONCHO? NDIDAMVA ZA ZOZIZWITSA ZANU.
MASEWERATU. MUNTHU AMENEYU WAKHALA ALI WOLUMALA KWA ZAKA 38.
LERO NDI SABATA LATHU LOYERA. ALIBE MPHAMVU ZOSOKONEZERA MTENDERE WATHU.

YOHANE 5:1–8

LUKA 14:5–6; YOHANE 5: 9–17



YOHANE 5:18–29

YOHANE 5:30-39, 45, 6:42-43, 7:25-32, 40-41

MATEYU 5:6, 9; YOHANE 4:14, 7:45-52

AMANAMIZA ANTHU WAMBA NDI BODZA LAKELO.
AONEKA KUTI ALI NDI YANKHO PA CHILICHONSE.
BWANJI TITUMIZE MMODZI MWA MALOYA OCHENJERA KWAMBIRI KUTI AKAMUSOKONEZE.
LOYA WOTERO NDIKUMUDZIWA. NDI WOCHENJERA KOMANSO ALIBE CHIFUNDO.
LOYA AKUBWERA KUDZAYESA YESU.
MALAMUL O AMATI CHIYANI?
MPHUNZITSI, NDICHITE CHIYANI KUTI NDIKAPEZE MOYO WOSATHA?
AMATI UZIKONDA AMBUYE MULUNGU WAKO NDI MTIMA WAKO WONSE, MOYO WAKO WONSE, MPHAMVU ZAKO ZONSE, NDI NZERU ZAKO ZONSE, NDIPONSO KUTI UZIKONDA MNZAKO MONGA MOMWE UMADZIKONDERA IWE MWINI.
WAYANKHA BWINO ZEDI. CHIKONDI NDICHO CHIMAKWANIRITSA MALAMULO ONSE. NGATI UKONDA MNZAKO MONGA MOMWE UMADZIKONDERA IWE MWINI, UDZAKONDWERETSA MULUNGU.
INDE, KOMA NANGA MNZANGAYO NDANI? MUKUTANTHAUZA ALIYENSE NGAKHALE AROMA, AKUNJA AJA?
NDIKUUZA NTHANO:
MUNTHU AMENE ANKACHOKERA KU YERUSALEMU KUPITA KU YERIKO ANAVULAZIDWA NDI ACHIFWAMBA PA NJIRA, ANAMUVULA ZOVALA ZAKE, NKUMUSIYA ATAKOMOKA.
PAMENE WANSEMBE ANKADUTSA NJIRA YOMWEYO, KUONA MUNTHU UJA ALI GONE, ANAMULAMBALALA NDIPO SANAIME KUTI AMUTHANDIZE.

LUKA 10:25-31

CHIMODZIMODZINSO MLEVI, MUNTHU WOSANKHIDWA KUTUMIKIRA M'NYUMBA YA MULUNGU, ANALAMBALALA NDIPO ANANGOIMA PATALI KWA KANTHAWI KOCHEPA KUYANG'ANA MUNTHU WOVULALAYO, KOMA SADAMUTHANDIZE.
KODI TINGAPINDULENJI KUNGONENA CHABE KUTI TIMAKONDA ANZATHU KOMA OSAONETSA NTCHITO ZA CHIKONDI? NGATI SUKONDA MNZAKO NDIYE KUTI SUKONDA MULUNGU.
KENEKA MSAMARIYA ANKADUTSA NJIRA YOMWEYO; MUNTHU AMENE AYUDA AMAMUNYOZA NKUMATI NDI WODETSEDWA. ATAONA MUNTHU WOVULALAYO, WOVULIDWA ZOVALA ZAKE, ALI GONE MU MSEU, SANALABADIRE ZOTI MUNTHUYO ANALI MYUDA.
MSAMARIYA ANAMUMVERA CHISONI, NDIPO ANAIMA KUTI AMUTHANDIZE.
MSAMARIYA UJA ANATSUKA ZILONDA ZA MUNTHU UJA NAZIMANGA NDI NSALU ZOMANGIRA ZILONDA. CHIKONDI CHAKE SICHINALI PA MAU CHABE, KOMA PA ZOCHITA.
KENAKA MSAMARIYA UJA ANAMUKWEZA MUNTHUYO PA BULU WAKE NAPITA NAYE KU MALO OTI AKASAMALIDWE, KOMWE ANAKAYENERA KUPUMA KUTI ACHIRE BWINOBWINO.
ZILI BWINO TSOPANO. NDAKUPEZA. POSACHEDWAPA UKAPUMULA POGONA PABWINO.
NDILIPIRIRATU NDALAMA ZA CHAKUDYA NDI MALO OGONA, NDALAMA ZA PA MILUNGU IWIRI. NGATI MTENGO WOMUSAMALIRA UKULIRAPO, NDIDZALIPIRIRA NDIKAMADZADUTSANSO POCHOKERA KOMWE NDIKUPITAKU.

LUKA 10:32-35

MATEYU 5:43-44; LUKA 10:36-37

MUTU 9:
ZOZIZWITSA NDI MAFANIZO

KWINA KWAKE KUDAALI MUDZI WA ANTHU AKHATE...
MASIKU AMBIRI APITAPO TSOPANO NDISANADYE CHILICHONSE.
UKUFA NGATI SUPHUNZIRA KUDYA MBEWA NDI TINYAMA TINA. KUDYA ZIMENEZI NDI NJIRA YOKHAYO IMENE TINGAKHALIRE NDI MOYO.
NDIYESA NDIKHALA WOYAMBA KUFA NDINE. CHAKA CHATHA CHOMWECHI NDINALI MUNTHU WOLEMERA KWAMBIRI; WOLEMEKEZEKA. TANGOONANI MOMWE NDILILI TSOPANO.
SUKULEMEKEZEKANSO TSOPANO; NDIWE WAKHATE, WOTAIDWA KUNJA.
POYAMBIRIRA NDINALI NDI CHIYEMBEKEZO CHOTI NDIDZACHIRA NDI KUBWERERA KWA MKAZI WANGA NDI ANA ANGA. KOMA NDAKHALA KUNO ZAKA KHUMI TSOPANO, NDIPO PALIBE AMENE NDAMUONA ATACHIRA NKUBWERERA KUMUDZI WAO.
POYAMBA MKAZI WANGA ANKANDIBWERETSERA ANA NDIPO ANKAIMA PATALI NKUMAYANKHULA NANE. KOMA KENAKA ANAYAMBA KUMABWERA KAMODZI PAKAPITA NTHAWI YAITALI. NDIYE KUTI ANA ANGA ANAKULA TSOPANO. ATANDIONA SANGANDIZINDIKIRE. NDI BWINO KUNGOFA BASI KUSIYANA NKUMAZUNZIKA CHOTERE.
AAA, LEKA KUDZIMVERA CHISONI. PALIBE AMENE AMASAMALIRA, NGAKHALE MULUNGU AMENE. TIYENI TIZIPITA TIKAYESE KUPEMPHAKO CHOTI TIDYE.
TIPITA KU MSEU WAUKULU LERO. TIKAONE NGATI ENA ANGATHE KUTICHITIRAKO CHIFUNDO.
NDI BWINO KUTI TIYENDERE LIMODZI. NDIKUONA ANTHU AKHATE PATSOGOLOPO.

NDIKUONA ANTHU APAULENDO MUMSEUMU!
TAONANI! NDI ANYAMATA OMWE AJANSO.
CHOKANI KUNO, ANTHU ODETSEDWA AKHATE. PITANI KWINA NDIPO MUKAFERE KOMWEKO.
INU MPHUTSI ZODETSEDWA! MULUNGU AKUKULANGANI.
THAMANGANI! THAMANGANI!
ODETSEDWA! ODETSEDWA, TONSEFE NDIFE ODETSEDWA.
NDI ANTHU AKHATE. MUSALOLE KUTI AKUYANDIKIRENI. ANGAKUPATSIRENI MATENDAWO.
TICHITIRENIKO CHIFUNDO. TIPATSENIKO CHAKUDYA, NGAKHALE CHOCHEPA, KUTI ALIYENSE WA IFE ALUMEKO.
APATSENI CHAKUDYA CHILICHONSE KUTI AZIPITA.
PITANI. INU ANTHU ODETSEDWA!
FUTUKANI KAYE NDIPO CHAKUDYACHO TICHISIYA PANO, PANSI.
MUSAYANDIKIRE. NDIYAMBE NDACHOKA KAYE.

BUREDI!
SUNGIRENIKO!
CHAKUDYA!
MUSAMALIZE CHONSE!
NDI CHANGA!
IWE CHIMGU BUDU!
BUREDI! BUREDI!
INU MULUNGU!
KUKUBWERA GULU LALIKULU LA ANTHU OYENDA MU MSEU.
TICHENJERE CHIFUKWA NDI ANTHU AMBIRI ZEDI.
NDIPO ONSEWO NDI AMUNA.


AMENEYO NDI YESU WA KU NAZARETI. NDINAMUONAPO KAMODZI NDISANAYAMBE KUDWALA MATENDAWA. IYEYU NDI AMENE AMACHIRITSA ANTHU.
AMATI NDI WOCHOKERA KWA MULUNGU. AMATI IYEYU NDI ATATE NDI AMODZI. NDIDAMUONA AKUCHIRITSA MUNTHU WAKHUNGU NDIPONSO MUNTHU WOLUMALA.
YESU! TITHANDIZENI!
AMBUYE, NDI ANTHU AKHATE.
MUSALOLE KUTI AKUYANDIKIRENI
MUFUNA NDIKUCHITIRENI CHIYANI?
MUTICHITIRE CHIFUNDO NDIPO MUTICHIRITSE.
NGATI MUFUNA, MUKHOZA KUNDICHIRITSA.
MUSANDIGWIRE.
MUSADE NKHAWA. PITANI KU NYUMBA YA MULUNGU NDIPO MUKADZIONETSE KWA WANSEMBE. AKAONA KUTI MWACHIRA NDIPO AKAKULOLANI KUBWERERA KUMUDZI KWANU; KU MABANJA ANU.
AKUTI TACHIRITSIDWA.
AKATITHAMANGITSA TISANAYANDIKIRE NYUMBA YA MULUNGU.
INE NDICHITA MONGA WANENERA.
INENSO NDICHITA NGATI IWEYO. TIYE TIZIPITA.

LUKA 17:11–14

YESU ANATI TACHIRITSIDWA.
NDIKUPEZA BWINO.
TIKUSINTHIKA!
KHUNGU LANGA LACHIRITSIDWA!
YESU NDIYE WACHITA ZIMENEZI! MWACHIRA!
SINDINUNSO ONYANSA!
NDIPITE KWA MKAZI WANGA!
WODALITSIKA NDINU, MWANA WA MULUNGU, MFUMU YA ISRAELE. MWANDIPATSANSO MOYO WANGA. MULUNGU NDI WACHIFUNDO NDI WACHISOMO.
KODI ANACHIRITSIDWA AJA SI ANTHU KHUMI? KOMA MMODZI YEKHA NDIYE WABWERA KUDZATHOKOZA, KOMANSO SI MYUDA. NDI MSAMARIYA.

LUKA 17:14-19

MATEYU 7:13-14, 22-23; CHIVUMBULUTSO 14:11

LUKA 16:19-22; AHEBRI 9:27

PAMENE MTEMBO WA MUNTHU WA CHUMA UJA UMACHOKA KUMUNDA KWAKE KUPITA KUMANDA, ANTHU ANAONA KUTI NAYENSO LAZARO WOPEMPHA UJA WAMWALIRA.
NDI **LAZARO,** MKULU WOPEMPHA UJA. NAYENSO WAMWALIRA USIKU WATHAWU. KOMA AKUONEKA KUTI WAFA MU MTENDERE.
THUPI LA LAZARO ANALINYAMULIRA PA NGOLO KUPITA NALO KUMALO KUMENE NYAMA ZAKUFA AMAZITAIRA, NKUZIOTCHA. SANACHITE MWAMBO WA MALIRO NDIPO PALIBE AMENE ANAMULIRA.

KOMA ANGELO ANABWERA NANYAMULA LAZARO KUPITA NAYE KU PARADIZO.
LAZARO, MBALE WATHU, TAKULANDIRA. SUDZAMVANSO NJALA NDIPO THUPI LAKO SILIDZAWAWA. BWERA, TAKUKONZERA CHAKUDYA.
EEE! ULENDO WABWINO BWANJI! SINDINKAGANIZA KUTI KUMWALIRA KUNGAKHALE KOSANGALATSA CHONCHI!

MUNTHU WACHUMA UJA ANAMUIKA MWAPAMWAMBA ZEDI M'MANDA ABWINO KWAMBIRI, NDIPO ALIYENSE AMENE ANKAKONDA NDALAMA ZAKE ANABWERA KUDZAONA CHIMENE ANAWASIYIRA M'CHIKALATA CHONENA ZA KAGAWIDWE KA KATUNDU.
ANALI MUNTHU WABWINO. INDE NTHAWI ZINA ANKAONEKA NGATI WOUMA MTIMA KWA AMENE ANKAWAKONDA, KOMA TIDZAMKUMBUKIRA NTHAWI ZONSE KUTI ANKAKONDA DZIKO LAKE NDIPONSO KUTI ANALI WACHILUNGAMO M'ZOCHITA ZAKE.
WAPITA KUKALANDIRA MPHOTHO YAKE. MZIMU WAKE UWUSE MU MTENDERE WOSATHA.

KOMA PAMENE MUNTHU WACHUMAYO ANAMWALIRA ANAPEZEKA KUTI ALI M'DZENJE LAKUYA KWAMBIRI.

LUKA 16:22

TATE WANGA **ABRAHAMU,** MUNDICHITIRE CHIFUNDO. NDIKUONA LAZARO KUMENEKO. MUUZENI KUTI ATENGE MADZI KU CHALA CHAKE NDIPO ADZAZIZIRITSE LILIME LANGA, POPEZA NDIKUVUTIKA KWAMBIRI NDI MOTO.

MWANA WANGA, NKADAKUTHANDIZA NDITHU NKADAFUNA, KOMA PALI PHOMPHO LALIKULU PAKATI PATHU, NDIPO PANSI PAKEPA PALI NYANJA YA MOTO. SITINGAOLOKE KUDZAKUTHANDIZA, NDIPO IWENSO SUNGAOLOKE KUBWERA TSIDYA LINO.

NDIPOTU MUMTUMIZE LAZARO KU NYUMBA YA BAMBO WANGA KUTI AKACHENJEZE ABALE ANGA KUTI ASADZAONE ZIMENE NDIKUONA INEZI M'MALO OZUNZA ANO.

ALI NDI ZIMENE MOSE NDI ANENERI ADALEMBA. ANGOKHULUPIRIRA MAU A MULUNGU.

KOMA ZIMENEZI SIZINGAWAKWANIRE. ATAONA CHOZIZWITSA CHOTI WINA WAUKA KWA AKUFA, AKHOZA KULAPA TCHIMO LAO LA KUSAKHULUPIRIRA.

NGATI SAKHULUPIRIRA MAU A MULUNGU, SANGATEKESEKE NGAKHALE ATAONA KUTI WINA WAUKA KUMANDA. WACHEDWA NAZO. ADZISANKHIRE OKHA. PEPA. PALIBE CHIMENE NDINGACHITE.

LUKA 16:22-31

EKSODO 20:14; LUKA 8:2; 1 YOHANE 1:9

LUKA 8:2, 11:24-26

MLALIKI 12:14; MATEYU 23:25, 6:19-21, 25, 28-30, 12:36; LUKA 15:1-3


MUNTHU WINA ADAALI NDI ANA AAMUNA AWIRI. MWANA WACHIWIRI ANALI WOSAMVERA NDIPO ANAFUNA KUKHALA MOYO WOMACHITA ZOMWE AKUFUNA.
EEE, NDIMAIKON DA NTHANO IMENEYI.
CHONCHO ANAFUNA KUTI ALANDIRIRETU CHOLOWA CHAKE.
ABAMBO, MUKANDIPATSA MBALI IMODZI YA MUNDA WANU NGATI CHOLOWA CHANGA, NDIPITA MU MZINDA KUKACHITA ZIMENE ZINGANDIPINDULIRE.
KOMA MWANA WANGA, ZONSE ZIMENE NDILI NAZO NDI ZAKO. INETU NDIFA POSACHEDWAPA NDIPO IWE NDI MKULU WAKO MUDZATENGA ZONSEZI KUTI ZIKHALE ZANU. MUDZAKHALA PABWINO MOYO WANU WONSE. TILI NDI NKHOSA NDI NG'OMBE ZAMBIRI. NDIPO TIMAKOLOLA ZOCHULUKA CHAKA NDI CHAKA CHIFUKWA MINDA YATHU NDI YACHONDE. TILI NDI ANTCHITO AMBIRIMBIRI NDIPONSO...
KOMA NDIKUFUNA KUTI NDICHOKE NDITHU KUTI NDIKAONE MMENE DZIKO LILILI. SINDIKUFUNA KUKHALA PAMUNDA PANO MOYO WANGA WONSE NDI KUMAGWIRA NTCHITO NGATI KAPOLO. NDILI MNYAMATA CHONCHI NDIFUNA NDISANGALALEPO. ANZANGA...
ANZAKO, AMENE SAGWIRA NTCHITO, AMANGOGANIZA ZOTI KODI HATCHI YOTHAMANGA KWAMBIRI NDI ITI, VINYO WABWINO KWAMBIRI NDI UTI, NANGA AKAZI OSANGALATSA KWAMBIRI NDI ATI.
KODI MUMADZIWA MMENE MOYO UMAKHALIRA? MUMANGOKHALA PHWII PA MUNDA WAKALEKALEWU. NDIKUFUNA MUNDIGAWIRIRETU MBALI INA YA MUNDA WANUWU TSOPANO LINO. NDIKUPITA KU MZINDA KOMWE NDIZIKAKHALA MONGA MOMWE NDIFUNIRA POPANDA WINA WONDISOKONEZA.
MPATSENI. TIDZAKHALA BWINOBWINO POPANDA IYEYU. PAJATU NTHAWI ZONSE SAGWIRA NTCHITO YOMWE WAPATSIDWA.
BAMBO UJA ADAMPATSA MWANA WAKEYO CHUMA CHIMENE ANKAFUNACHO. CHONCHO MWANAYO ANACHOKA, NAOLOKA NYANJA, KUPITA KU MIZINDA IKULUIKULU KUMENE ANKATI AKAPEZAKO CHISANGALALO.
TSOPANO UKU NDIKO KUKHALA – PALIBE WINA WONDIUZA ZOCHITA.

LUKA 15:11–13

MWANA WAMNG'ONO...
EYAA, IZI NZABWINO KUPOSA MMENE NDINKAGANIZIRA. TAONANI ANTHU ONSEWA NDIPONSO NYUMBA. KUNO NDIYE KUCHIMAKE KWA CHISANGALALO.
NDIYENERA KUPEZA MALO OGONA ABWINO KWAMBIRI OMWE NDIZILIPIRA.
EYAA, IYI IKUONEKA YABWINO KOPOSA. NDIZIKHALA M'MENEMU.
NGATI MUFUNA TIKUTHANDIZENI MUNGOTIFUNSA. TIMATUMIKIRA USANA NDI USIKU WOMWE.
NDANINSO AMENE ANGAFUNE MALO ENA OPOSA AWA? MAWA NDIPITA KUKAKUMANA NDI ANTHU ENA MUMZINDAMU.

LUKA 15:13

EEI, NDANI UYU? MNYAMATA WACHIMIDZIMIDZI. TITAONA NKHOPE YAKE, ANGAONEKE KUTI NGOKONGOLA.
EEI, MNYAMATA, NGATI UKUFUNA KUTI USANGALALE NAFE, NDI BWINO KUTI UMETE KAYE NDEVU ZAKOZI NDIPONSO UPEZE ZOVALA ZABWINO OSATI ZIMENE WAVALAZI.

TADZIONA. UKUONEKA BWIN NDI ZOVALA ZATSOPANOZI.

TAKONDWA KUTI ULI NAFE PAMODZI PA CHAKUDYA CHAMADZULOCHI.
AKUONEKATU BWINO TSOPANO CHIFUKWA WACHOTSA NDEVU ZIJA. SICHONCHO?

TILANDIRE MNZATHU WATSOPANOYU. NTHAWI ZONSE AZIPEZA CHISANGALALO NDI CHIMWEMWE.
...NDI CHIKONDI.

MNYAMATA, BWERETSA VINYO WINANSO KUTI ANZANGA AMWE.

LUKA 15:13

KODI SITINGAPITE KUMENE UMAKHALA, IWEYO NDI INE?
CHONCHO MNYAMATA UJA, KUTALI NDI KWAO, ANAKHALA ALI NDI NDALAMA KWA MIYEZI YAMBIRI NDITHU. PAMENE ADALI NDI NDALAMA, ANALINSO NDI ABWENZI AMBIRI.
TSIKU LINAFIKA PAMENE CHISANGALALO CHAKECHO CHIDAMUTHERA NDALAMA ZONSE – KOMA ADALI NDI ABWENZI AMBIRI AMENE ANALI OLEMERA KWAMBIRI.
UKAMATI ULIBE NDALAMA UKUTANTHAUZA CHIYANI? KODI SUJA UDAALI WOLEMERA?
ZOONADI, KOMA KUKHALA KUNO PAMAFUNIKA NDALAMA ZAMBIRI, NDIPO NDALAMA ZIMENE ZIDANDITSALIRAPO NDINATHERA NJUGA SABATA LATHA. NDIMAGANIZA KUTI NDIPAMBANA NJUGAYO, KOMA...
UKUTANTHAUZA CHIYANI UKATI ULIBE CHILICHONSE? NANGA DERESI LIJA UDANDILONJEZA UNDIGULIRA BWANJI?
NDIMAYEMBEKEZA KUTI ABAMBO AKO ANDILEMBA NTCHITO YOSAMALIRA CHUMA CHAO?
NTCHITO?
SINDIKUKHULUPIRIRA KUTI NDIKUDYETSADI NKHUMBA – NYAMA ZODETSEDWA, ZAUVE.
NDIMAGANIZA KUTI NDILI NDI ABWENZI. SANDIYANKHULITSANSO TSOPANO. KOMA NDIPEZA NTCHITO INA NDIPO NDIDZALEMERANSO.
MHU
MHU
MHU

LUKA 15:13-15

SINDILABADAKO ZA MMENE WADWALIRA. DZUKA PAMENEPO KUTI UKASAMALE NKHUMBA. NDIKUCHOTSA NTCHITO NDIPO NDILEMBA WINA. NYAMUKA TSOPANO LINO!
INDE, BWANA, PEPANI. NDIKUPITA POMPANO, BWANA.
NDALAMA ZIMENE NDIMALANDIRA POGWIRA NTCHITOYI NDI ZOCHEPA KWAMBIRI NDIPO SINDIDYA BWINO. NDIGANIZA KUTI ANZANGA AJA NDINKASANGALALA NAWO AKUDYA BWINO.
ONANI MOMWE NDILILI TSOPANO. NDIKUMVA KUZIZIRA, NDILI NDI NJALA, KOMANSO NDATOPA. NDIKHOZA KUDYA CHAKUDYA CHANKHUMBACHI. ANTCHITO A ABAMBO ANGA ALI NDI CHAKUDYA CHOCHULUKA KWAMBIRI NDIPO AMADYA MOMWE ANGATHERE. NDIKADAPITA...KOMA IYAYI, SINDIKUFUNA NDITABWERERA, SINDIDACHOKE BWINO. AKHOZA KUKANDINYOZA.
NDASANDUKA WOPUSA KWAMBIRI. NANGA NDITABWERERA NDIKUKAWAPEMPHA KUTI NDIKHALE WANTCHITO WAO? NDIDAMALIZA CHOLOWA CHANGA CHONSE. KOMA NDIKHOZA KUKAKHALA WANTCHITO – AKAKANDILANDIRA.
NDIKUPITA KWATHU.
WOPUSA IWE! ULIBE NDALAMA. UYENERA KUYENDA MTUNDA WAUTALITALI KUTI UKAFIKE KWANUKO.
ATAYENDA KWA MILUNGU INGAPO, ANAYANDIKIRA KWAO.
NDAKHALA PANG'ONO KUFIKA. NDILIBE MPHAMVU ZOKAPEMPHERA KUTI ANDICHITIRE CHIFUNDO. NDIKANENA KUTI, "ATATE, NDAKUCHIMWIRANI NDIPO SINDIYENERANSO KUTCHEDWA MWANA WANU. MUZINDIONA INE NGATI MMODZI MWA ANTCHITO ANU."

LUKA 15:16–19

MUKUMUONA MUNTHU AMENE AKUBWERA APOYO? MASO ANGAWA ADAKALAMBA NDIPO SAONA MONGA KALE, KOMA AKUYENDA NGATI MWANA WANGA AMENE ADALOWERERA KALEKALE.
INDE, NDI WOKULIRAPO, NDIPONSO WOWONDA, KOMA NDIKUKHULUPIRIRA KUTI NDI MWANA WANU.
MWANA WANGA!
MWANA WANGA, MWANA WANGA, WAFIKA KWANU!
ATATE, NDAKUCHIMWIRANI...
...NDIPO SINDIYENERA KUTCHEDWANSO MWANA WANU.
TIMAYESA KUTI UDAMWALIRA, KOMA UKADALI NDI MOYO. TIYENERA KUKUSAMALA POMPANOPOMPANO.
SUNGAPITE KU NYUMBA MMENE UKUONEKERAMU. WANTCHITO WANGA ABWERETSA CHOVALA CHABWINO NDI NSAPATO ZOTI UVALE KUPHAZI KWAKOKU. MPHETE YAKO IJA IDASOWA. INDE, UYENERA KUKHALA NDI MPHETE. MWANA WANGA AMENE ADATAYIKA TSOPANO WAPEZEKA.

LUKA 15:20–22

IPHANI MWANAWANG'OMBE WONENEPA BWINO, KONZANI PHWANDO, ITANANI ANTHU, KUTI TISANGALALE, PAKUTI LERO NDI TSIKU LOTI TIKONDWERE.
NDAKONDWA KUTI NONSENU MULI PANO KUDZASANGALALA NDI INE PA CHIKONDWERERO CHINO. MWANA WANGA AKADALI WOFOOKA CHIFUKWA CHA ZIMENE WADUTSAMO, KOMA CHIFUKWA CHA CHAKUDYA CHABWINO AKHALANSO WAMPHAMVU POSACHEDWAPA. LERO NDI TSIKU LOPAMBANA PA MOYO WANGA.
MWANA WAMKULU ADAACHOKAPO KWA MASIKU AMBIRI NDITHU. ATABWERERA KU MUDZI, ANAPEZA PHWANDO LILI M'KATI.
NANGA NYIMBOZI NDIPONSO KUVINA KUMENE NDIKUMVA?
MNG'ONO WANU WABWERERA KWAO KUNO ALI WOMVETSA CHISONI. AKUDWALA NDIPONSO NDI WOSAUKA. ATATE ANU AKUKONDWERERA CHIFUKWA CHOTI MNG'ONO WANUYO WABWERA. FULUMIRANI KULOWA M'KATIMO.
SINDINGACHITE NAWO ZOPUSAZO. IYEYU WAKHALA M'MOYO WOCHIMWA NDI WOCHITITSA MANYAZI.
WANTCHITO UJA ANAKAUZA ATATEWO ZOMWE MWANA WAO WAMKULU ADANENA, NDIPO ANATULUKA KUDZAYANKHULA NDI MWANA WAKEYO.
KWA NTHAWI YAITALI NDAKHALA NDIKUMUFUNAFUNA, NDIMAYESA KUTI ADATAYIKIRATU. NDIDAKHALA PANG'ONO KULEKA KUMFUNAFUNA KOMA PANO WABWERA. UNGALIMVETSE DALITSO LIMENELI? MULUNGU NDI WABWINO!
SINDIKUMVETSA CHIFUKWA CHOMWE MUKUKONDWERA NDI MUNTHU WOCHIMWAYO. INE SINDIKONDWERA NAWO ZIMENEZI.
NTHANO IMENEYI NDI YOSANGALATSA. KOMA KODI UKUGANIZA KUTI IFE TILI NGATI MWANA WAMKULU UJA?
AMENE ALI NDI MAKUTU, AMVE.

LUKA 15:23-32

MATEYU 20:17–20; YOHANE 11:11–15

YOHANE 11:17–31

YOHANE 11:32-42

YOHANE 11:43-44



YOHANE 11:44-28



MATEYU 10:22, 24:2, 5-9, 27-31; LUKA 19:43-44, 21:8; YOHANE 11:49-53; CHIVUMBULUTSO 2:10

MATEYU 20:19, 26:2; YOHANE 12:1–2, 14:6

MATEYU 20:19; YOHANE 12:3-8, 10:11

YOHANE 12:12–13

MATEYU 21:11–12

MASALIMO 69:9; MATEYU 21:12–13

MATEYU 26:14-16; MARKO 13:5-13; LUKA 17:26-37; YOHANE 12:23-24; 2 PETRO 3:10

YOHANE 12:27-36

MUTU 10:

PASKHA NDI MASAUTSO A KHRISTU

PITANI, KAKONZENI PASKHA KUTI TIDYE.

NDAFUNA KUTI NDIDYE NANU PASKHA UYU NDISANAYAMBE KUZUNZIKA. SINDIDZADYANSO PASKHA WINA KUFIKIRA UFUMU WA MULUNGU UTAKHAZIKITSIDWA PA DZIKO LAPANSI. PAMENEPO MUDZADYA PA TEBULO LANGA, NDIPO MUDZAKHALA PA MIPANDO KUWERUZA MAFUKO KHUMI NDI AWIRI A ISRAELE.
NDIKUUZANI CHINTHU CHINA, KUTI CHIMENECHO CHIKACHITIKA MUKHULUPIRIRE. MAU A MULUNGU PA MASALIMO 41:9 AKUTI, "IYE AMENE ADYA NANE MKATE, WANDIKWEZERA CHIDENDENE CHAKE." NCHIFUKWA CHAKE NDIKUKUUZANI KUTI MMODZI WA INU AMENE DZANJA LAKE LILI NDI INE PA TEBULO LINO ADZANDIPEREKA KWA ADANI.
ZOSATHEKA!

IZI ZAKHAZIKITSIDWA KUTI ZITERO NDITHU, KOMA TSOKA KWA MUNTHU AMENE ADZACHITA CHINTHU CHIMENECHI.


AMBUYE KODI NDINE? INE SINDIKUFUNA KUKUPEREKANI KWA ADANI.
AMBUYE, SINDINE, SICHONCHO?
AMBUYE, SINDINGAKUPEREKENI.

LUKA 22:8-23

MATEYU 26:23-29; YOHANE 13:26-30

MATEYU 26:33-35; YOHANE 13:31-38; I AKORINTO 11:24-25

YOHANE 14:1-3; 1 AKORINTO 11:24-26

MATEYU 26:30; YOHANE 14:5-10, 15, 25-30

MATEYU 26:31, 38; YOHANE 16:19–20, 17:1–10

MASALIMO 23:5-6; LUKA 22:41-44; AHEBRI 6:6; 12:2

MATEYU 26:40, 45-50; YOHANE 12:27, 18:1-4

YOHANE 18:4-6, 10

MATEYU 26:52–57; MARKO 14:51–52; LUKA 22:50–51

YOHANE 18:19-23

MATEYU 26:59-65

MATEYU 26:67-70; LUKA 22:64-65

MATEYU 26:71–75, 27:1–2; LUKA 22:58–62, 23:1

MKWAPULENI NDI MKWAPULO WA MINGA ZISANU NDI ZIWIRI.
MULUNGU, NDAPHULAPO CHIYANI. NDAMUKANA KATATU, MONGA MOMWE ADANENERA. ZACHITIKIRANJI ZIMENEZI? AKUZUNZIKIRANJI?
FULUMIRANI. KUNJA KUKUCHA.
ATATE, PATSENI MPHAMVU.
UKUFUNA CHIYANI TSOPANO? KODI NDALAMA ZIMENE TINAKUPATSA CHIFUKWA CHOPEREKA MBUYE WAKO SIZIDAKWANE?
NDASINTHA MAGANIZO. MUITANITSENI KUTI MUMUMASULE NDIPO NDIDZAKUBWEZERANI NDALAMA ZANU.
ZIMENEZO NDI NDALAMA ZA MAGAZI, ZODETSEDWA; SITINGAZIKHUDZE. MBUYE WAKO APHEDWA LERO LINO BASI. USAOPE CHILICHONSE. TIDZAKUGWIRITSA NTCHITO YOGWIRANSO OPHUNZIRA ENA AJA KUTI TITHANE NAWO.
TENGANI NDALAMA ZANU. SINDIKUZIFUNA. SINDIKUPEZA MTENDERE MUMTIMA MWANGA.
NGWIII!
NGWIII!
WOPUSA.
SINDINGAKHALE MOYO CHIFUKWA CHA ZIMENEZO.

MATEYU 27:3-6

MULUNGU, VUTO LANGA NCHIYANI?
NCHIFUKWA CHIYANI SINDIDADZILETS E UMBOMBO WANGAWU.
MWINA IMFA IKHOZA KUNDIPATSA MTENDERE...
NDINAMUONA KOMA PALIBE CHIMENE NDIKANACHITA POFUNA KUMULETSA.
FULUMIRANI, TIDULE CHINGWECHO; MWINAMWAKE AKADALI NDI MOYO!
KOMA PAMENE ANKAKWERA MUMTENGOMO, MZIMU WA YUDASI UNALI UTAFIKA KALE M'MOTO WA CHIONONGEKO.
AKAMAGWA MUMUGWIRE KUTI ANGAGWERE KUPHOMPHO.

MATEYU 27:5

ZEKARIYA 11:12–13; MATEYU 27:8; MARKO 15:14; LUKA 23:1–4; YOHANE 18:29–38; NTCHITO 1:18

LUKA 23:11; YOHANE 19:1

MSANA WAKE WAONONGEKERATU!
EYA, NTHAWI YONSEYO NDIMALAKALAKA NTAMENYAPO MFUMU.
ANKATI IYEYU NDI MFUMU. MVEKENI CHOVALA ICHI.
MFUMU IMAYENERA KUKHALA NDI CHISOTI CHAUFUMU.
HA HA HA ICHI CHINGAKHALE CHISOTI CHAUFUMU CHABWINO.
OOO!
ICHO, TENGANI CHISOTI CHANU, INU WAMKULUKULU. HA HA HA.
MUIKE BWINOBWINO CHISOTICHO PAMUTU PAKEPO.
TIKUKUVEKANI CHISOTI CHAUFUMU INU MFUMU YA DZIKO LONSE LAPANSI.
AAAAAAA!
TSOPANO, IMIRIRA BWINOBWINO MOONGOKA.
GWIRITSITSANI CHISOTI CHANU, MFUMU.
HA, HA, MUKHALE NDI MOYO WAUTALI, MFUMU.
INDE, NGAKHALE KUTI AFA USIKU WOMWE UNO.

YOHANE 19:1-3

LUKA 23:13-22; YOHANE 19:4-8

MATEYU 27:24; YOHANE 19:9-17

MATEYU 27:32; LUKA 23:26–33

MATEYU 27:33-34

ZEKARIYA 13:6; LUKA 23:32-34

MASALIMO 22:18; MATEYU 27:39-43; YOHANE 19:23-24

MASALIMO 69:21; LUKA 23:36-43; YOHANE 19:25-27

MATEYU 27:45-50; LUKA 23:44-46; YOHANE 19:30; 2 AKORINTO 5:21

MASALIMO 34:20; ZEKARIYA 12:10; MATEYU 27:54; YOHANE 19:31-37

YOHANE 19:31, 38

MUTU 11:

KUUKA KWA AKUFA NDI MPINGO WOYAMBIRIRA

MATEYU 27:59-66; YOHANE 19:40

MATEYU 28:1–2; LUKA 24:1

NDI CHIVOMEZI CHACHIKULU KWABASI.
TAMVERANI MMENE ANTHUWO AKUFUULIRA! NKUTHEKA KUTI WINA WAVULALA.
CHIYA...?
AAAA!
NDI MULUNGU!
AKUCHOTSA MWALA!
ATIPHA!
MULUNGU, TICHITIRENI CHIFUNDO!
MUSANDISIYE! CHITIRENI CHIFUNDO MULUNGU!
TAONANI!
THAWANI!

MATEYU 28:2-4

MWALA UMENE UJA NDI WAUKULU KWAMBIRI. ANTHU OTI AKATICHOTSERE MWALAWO TIKAWATENGA KUTI?
SINDIKUDZIWA, KOMA WAKHALA PAMENEPO MASIKU ATATU. POPANDA ZONUNKHIRITSA, MTEMBOWO WAYAMBA KUNUNKHA TSOPANO.
SADADZIWE KUTI ASILIKALI ANKALONDERA MANDAWO.
PATAPITA MPHINDI ZOCHEPA
WINA WACHOTSA KALE MWALA UJA!
THUPI LAKE LABEDWA BASI. M'MANDAMO MULIBE!
OO! INU NDINU YANI? MTEMBO WA YESU ULI KUTI?
NSALU ZOIKIRA MALIRO ZIJA NDI IZO ZILI APOZO!
MUSAZIZWE. NDIKUDZIWA KUTI MULI KUFUNA YESU, AMENE ADAAPACHIKIDWA PA MTANDA. WAUKA MONGA MOMWE ADANENERA.
BWERANI MUDZAONE POMWE ANAGONEKEDWA, NDIPO PITANI MUKAUZE OPHUNZIRA AKE KUTI YESU AKAKUMANA NAWO KU GALILEYA.
YESU ALI NDI MOYO! MUKUTI WAUKA KWA AKUFA; MONGA LAZARO!
AMENEWO NDI ANGELO!
YESU ALI NDI MOYO!
TIFULUMIRE, TIKAWAUZE OPHUNZIRA AKE.

MARKO 16:3-8

YESU ALI NDI MOYO. PANOPA TIKUCHOKERA KUMANDA.
YESU MULIBE M'MANDAMO, KOMA TINAPEZAKO ANGELO.
TINAKUMBUKIRA KUTI YESU ANATI ADZAUKA PA TSIKU LACHITATU.
ANGELOWO AKUTI YESU AKAKUMANA NANU KU GALILEYA!
PETRO, UKUPITA KUTI?
KUMANDA.
YOHANE ANAMUTSATIRA, NDIPO YOHANEYO ANAPITIRIRA PETRO.
YOHANE! DIKIRE; SINDINGATHAMANGE MONGA IWEYO.
MULIBE!
ZIMENEZI ZIKUTANTHAUZA CHIYANI?

YOHANE 20:2-6

YOHANE 20:7-17

MASALIMO 22; ZEKARIYA 13:7; LUKA 24:13-26



MASALIMO 11:4, 22:15, 41:9, 42:4,6, 45:23, 49:6, 52:13; YESAYA 7:14,16, 9:6, 11:1, 40:11, 42:7, 49:7, 53:1,3, 59:20; YEREMIYA 23:5-6; MIKA 5:2; ZEKARIYA 11:12-13, 12:10, 13:6-7; YOHANE 10:18

KWATHU NDI KUNO. CHONDE BWANA, KWADA. BWERANI MUGONE KUNYUMBA KWATHU KUNO. NDIFUNA NDIMVE UNENERI WAMBIRI WOKHUDZA YESU.
AKULU, ZINGAKHALE BWINO KWAMBIRI MUTAPEMPHERERA CHAKUDYACHI.
WODALITSIKA NDINU AMBUYE MULUNGU WATHU, MFUMU YA DZIKO LONSE, AMENE MUMATIPATSA CHAKUDYA KUCHOKERA M'NTHAKA. CHIFUKWA CHA CHAKUDYA ICHI, TIKUKUTHOKOZANI.
TENGANI, IDYANI.
YESU! NDIWEYO
AMBUYE!
WASOWA!
WAPITA!
KODI ANALI YESU, NTHAWI YONSEYI OSAMUZINDIKIRA!
NCHIFUKWA CHAKE AMADZIWA UNENERI WONSE UJA.
YESU NGWAMOYO! IMFA YALEPHERA KUMMANGA! NGWAMOYO! TIYENI TIBWERERE KU YERUSALEMU KUTI TIKAWADZIWITSE OPHUNZIRA ANZATHU.

LUKA 24:28-32



YOHANE 20:26-31; LUKA 24:36-43



MATEYU 28:18-20; LUKA 24:44-49; YOHANE 14:2-4

LUKA 24:49–51; MACHITIDWE 1:7–11



MACHITIDWE 1:12–14, 2:1–13, 32, 36

MASALIMO 2, 16:2; MACHITIDWE 2:27, 37–41

MACHITIDWE 3:1–11



MACHITIDWE 3:12, 14-19, 4:1-3

MACHITIDWE 4:3-6

MASALIMO 118:22; MACHITIDWE 4:7–21

MACHITIDWE 13:30–32, 4:10



YESAYA 66:1; MACHITIDWE 7:1–57

MACHITIDWE 7:58-59

MACHITIDWE 7:59-8:3

MACHITIDWE 8:26–29

MACHITIDWE 8:27, 30-34

YESAYA 53:3–10; MACHITIDWE 8:35; AROMA 2:16; 2 AKORINTO 5:21.

MASLIMO 22:6, 17–18, 16:10, 34:20; YESAYA 50:6; ZEKARIYA 12:10

MACHITIDWE 8:36-39

MUTU 12:

KU DZIKO LONSE LAPANSI

MATEYU 16:24; MACHITIDWE 9:1-2

MACHITIDWE 9:3-6

MACHITIDWE 9:7–19

MACHITIDWE 9:20-22, 10:1-27, 38-41

MASLIMO 2:7, 16:10; MACHITIDWE 2:27, 10:47, 13:35

MACHITIDWE 14:18–19

KOMA MULUNGU ANACHITA CHOZIZWA NDIPO ANAMUUTSA PAULO UJA.

PAULO, NDIMAGANIZA KUTI *WAFA!*

AI, NKADALI MOYO. MULUNGU ANANDIONETSA ZINTHU ZAMBIRI KUTI NDIDZAZUNZIKA CHIFUKWA CHA DZINA LAKE, NDIPO ICHI NCHIYAMBI CHABE. TIYE TIBWERERE MUMZINDAMO.

MWAYENERA, AMBUYE, KULANDIRA ULEMERERO, ULEMU NDI MATAMANDO...

KU FILIPI WA KU MASEDONIYA, PAULO NDI SILA ANAKWAPULIDWA MIKWAPULO 39, KENAKA NKUWATSEKERA M'NDENDE. POSALABADIRA MASAUTSO AO, MITIMA YAO INADZAZA NDI CHIMWEMWE, NDIPO PAKATI PA USIKU ANAYAMBA KUYIMBA NYIMBO ZOTAMANDA MULUNGU.

AAAAA! YESU NDI AMBUYE!

HWAPU!

PAULO ANAMENYEDWAPO KATATU NDI NDODO PA ZAKA ZINA ZITATU. KOMABE SANASIYE KULALIKA YESU.

MACHITIDWE 14:20, 16:23-25; 2 AKORINTO 11:24-25; CHIVUMBULUTSO 4:11

1 AKORINTO 10:14, 12:12–13, 18; 2 AKORINTO 11:25; AGALATIYA 2:6; AEFESO 2:19

YESU ADACHENJEZERATU OPHUNZIRA AKE KUTI, "ADZAKUPEREKANI KUTI AKUZUNZENI, NDIPO ADZAKUPHANI: ANTHU ONSE ADZADANA NANU CHIFUKWA CHA DZINA LANGA. AMBIRI ADZAKHUMUDWA NANE NDIPO ADZAPEREKA ANZAO KWA ADANI, NDIPONSO ADZADANA NDI ANZAOWO. ANENERI AMBIRI ONYENGA ADZAONEKA, NDIPO ADZANAMIZA ANTHU AMBIRI."

PAMENE ANTHU AMENE ADAONA YESU ANALI KUKALAMBA, NTHAWI IMENE MPINGO UDAFALA MU UFUMU WONSE WA AROMA, AROMA ADAYAMBA KUFUNAFUNA AKHRISTU NDI KUYAMBA KUWAZUNZA MWANKHANZA MPAKA KUMAPHA ENA MWA IWO. OKHULUPIRIRA AKAPANDA KUKANA KHRISTU, ANKAWAIKA M'BWALO LA ZAMASEWERO, NDIPO ANTHU ANKAONENERA MIKANGO NDI AKAMBUKU ZIKUWADYA OKHULUPIRIRAWO.

AMBUYE YESU, LANDIRANI MZIMU WANGA!

ATATE, MUSAWALANGE CHIFUKWA CHA ZIMENE AKUTICHITIRAZI.

GIGIRIIII!

EEEEI

NTHAWI ZINA AKHRISTU ANKAPHEDWA NDI ASILIKALI ACHIROMA. ANTHU ANKADABWA POONA KUTI OKHULUPIRIRAWO ANKAKANGAMIRABE YESU. ANALI OKONZEKA KUFA CHIFUKWA CHA YESUYO.

YASONI, TIKAONANA KU PARADIZO.

AAA!

MATEYU 24:9-11

YESU ASANAFE, ADANENERATU ZA TEMPILE:

KODI MUKUIONA TEMPILEYI? NDIKUKUUZANI KUTI IDZAONONGEKA NDIPO PALIBE MWALA UMENE UDZAKHALA PA UNZAKE.

ZAKA 40 PAMBUYO PA UNENERI WA YESU UJA, M'CHAKA CHA 70 A.D., AROMA ANAONONGA TEMPILE PAMODZI NDI MZINDA WA YERUSALEMU. MATABWA ATAYAKA M'KATI MWA TEMPILEYO, GOLIDE WA MU TEMPILE ANASUNGUNUKA, NKUMAYENDERERA M'MING'ALU PAKATI PA MIYALA YAPANSI NDI YAM'MAZIKO. PAMENE AROMA ANAFUNA KUDZATENGA GOLIDE WA MU TEMPILE UJA, ANAONA KUTI KUNALI BWINO KUTI AGUMULE TEMPILEYO. MAU A YESU ANAKWANIRITSIDWADI.

MATEYU 24:2; LUKA 19:43-44

MATEYU 14:10; YOHANE 21:18

1 ATESALONIKA 4:14, 16–17; 2 ATESALONIKA 2:2–3; CHIVUMBULUTSO 1:9, 11, 8:1–13, 9:18, 13:16, 20:4

1 ATESALONIKA 4:16; CHIVUMBULUTSO 1:16, 19:11–21, 20:10–15, 21:1–4



UTHENGA WABWINO WONENA ZA YESU KHRISTU NDI WOSIYANA NDI ZIPEMBEDZO ZINA ZA PA DZIKO LAPANSI, CHIFUKWA UTHENGAWU SUFALA CHIFUKWA CHA NKHONDO KAPENA CHIFUKWA CHOOPSEZA ANTHU. YESU ANAPHUNZITSA OMUTSATIRA KUTI AZIKONDA ADANI AO NDI KUTINSO AZIKONDWA NDI KUMAYIMBIRA MULUNGU. LERO LINO, ANTHU AMBIRI A M'MAIKO ONSE PA DZIKO LAPANSI AKUKONDWA CHIFUKWA CHAKUTI MULUNGU ADAWAKHULULUKIRA MACHIMO AO NDI KUTINSO ALI NDI MOYO WOSATHA.

KOMABE, PAPITA ZAKA PAFUPIFUPI 2000 KUCHOKERA PAMENE YESU ADAUKA KWA AKUFA, NDIPO PALI ENA AMENE SADAMVEPO UTHENGA WABWINO. PAFUNIKA KUTI WINA AWAUZE.

YOHANE 3:16, 14:6

M'CHAKA CHA 1999, AKHRISTU ENA AMENE AMAKHUDZIDWA KUTI ANTHU ENA SANAMVE UTHENGA WABWINO, ANAKUMANA NAKAMBIRANA ZA MMENE ANGAFALITSIRE UTHENGA WABWINOWU KWA ANTHU A ZINENERO ZOSIYANASIYANA PA DZIKO LAPANSI.
ANAGWIRIZANA KUTI NJIRA YABWINO NDI YOLEMBA BUKU LOKHALA NDI ZITHUNZI ZA NKHANI ZA M'BAIBULO MWA NJIRA YAKUTI ANTHU ONSE ATHE KUMVA BWINOBWINO UTHENGA WA YESU.

ATALEMBA NKHANI ZA M'BAIBULOZO, ANAPEZA MUNTHU WINA WOTCHEDWA DANNY BULANADI, MMODZI MWA ANTHU OTCHUKA KWAMBIRI PA DZIKO LAPANSI POLEMBA NKHANI M'ZITHUNZI, NDIPO ANAGWIRIZANA NAYE KUTI AJAMBULE ZITHUNZI (ZIMENE ZILI M'BUKU LINO).

KULEMBA, KUJAMBULA ZITHUNZI, NDI KUSINDIKIZA BUKU LINO KUNATENGA ZAKA ZISANU NDI ZIWIRI.
PANOPA BUKULI LIKUTANTHAUZIDWA NDI KUPEREKEDWA KWA ANTHU A ZINENERO ZOSIYANASIYANA PA DZIKO LAPANSI. AKHRISTU OKHUDZIDWA NDIWO AMENE AMAPEREKA NDALAMA ZAO KUTI BUKULI LIGWIRE NTCHITO IMENE LINALEMBEDWERA.

AKHRISTU ENA AKUPEREKA NDALAMA NDI MPHAMVU ZAO KUTI BUKULI LIFIKIRE ANTHU AMENE SANAMVE UTHENGA WABWINO WA YESU.
ULI BWANJI MNZANGA? NDILI NDI BUKU LIMENE NDIFUNA NDIKUPATSE. LIMANENA ZA MMENE MACHIMO AKO ONSE ANGATHE KUKHULULUKIDWIRA, NDI MMENENSO UNGAPITIRE KU PARADIZO UKAMWALIRA.
SINDINGAKWANITSE KUGULA BUKU LIMENELI.
SINDIKUGULITSA. NDI MPHATSO.

BWANJI MUKUNDIPATSA CHINTHU CHAULERE?
NCHIFUKWA CHAKUTI NDIMAKUKONDANI, ACHIMWENE, TERE LANDIRANI BUKULI.
NDILIWERENGA KUTI NDIONE NGATI PALINSO UTHENGA WINA UMENE WATSALA M'DZIKO LAPANSILI.

MMAWA MWAKE.
CHIPEMBEDZO CHANGA SICHINANDIUZEPO ZA ZIMENEZI. CHIMENECHI NDI CHIKONDI NDI CHIKHULULUKIRO.
NDIKUDZIWA NDI ZOONA! NDACHIMWIRA MULUNGU, KOMA ANATUMA MWANA WAKE KUDZAFERA MACHIMO ANGA! ZODABWITSA NDITHU!

AROMA 3:23, 6:23, 10:9

MACHITIDWE 19:2-5; AROMA6:3-4

MACHITIDWE 8:37, 4:10–12; AROMA 10:9

YOHANE 15:20; MATEYU 5:11-12

TIFULUMIRE; NYUMBAYI ITIGWERA POSACHEDWAPA!
MOHAMEDI ANAOMBOLA MBALE WAKE AMENE ANALI PA MOTO.
PAMENE MOHAMEDI ANKATI ABWERERE KU NYUMBA IMENE INKAYAKA MOTO IJA KUKAPULUMUTSA ABALE ENA...
KHWAA!
HUWUU
NYUMBA YAWAGWERA ONSEWO!
WAMWALIRA AKUTUMIKIRA CHIPEMBEDZO CHATHU. TILANGA AKHRISTU CHIFUKWA CHA CHIMENECHI.
WANSEMBEYO ANAMUIKA M'MANDA MWACHISONI NDI MANTHA, CHIFUKWA ANALIBE CHIYEMBEKEZO CHA MOYO WOSATHA.
MOHAMEDI ANAFA CHIFUKWA CHOFUNA KUTHANDIZA ABWENZI AKE. CHIKONDI CHOTERE NCHOPOSA.
AMAI, MUSADANDAULE. ABAMBO ALI NDI YESU NGAKHALE TSOPANO LINO.

YOHANE 15:13

MATEYU 7:21-27, 25:21, 25:30; 1 AKORINTO 6:9-11; YAKOBO 4:11-17